


# MIBADWO ISANU NDI IWIRI YA MPINGO

 ...Ambuye Yesu wodala. Ndipo ndi ziyembekezere zazikulu ine ndikuyang'anira ku mausiku awa a msonkhano, ndikudalira kuti mulimonse, mwanjira inayake, kuti Atate athu Akumwamba amwetulira madalitso Ake kwa ife. Ndipo nthawi zambiri ine ndimapeza mwayi wobwera muno kudzakhala ndi misonkhano iyi kuno mu—mu tchalitchi, ndi gululi, inu achichepere, gulu limene ndi mamembala pano a tchalitchi, ndi alendo, ndithudi.

<sup>2</sup> Ndipo uwu sunalengezedwe. Iwo unangokhala msonkhano wa mapemphero wa nthawizonse wa Lachitatu usiku. Ndipo ine ndinati, “Mwinamwake usikuuno tifufuza ngati tingabwerere.” Ndipo ine ndimaganiza kuti ife tiyisunthire iyo mtsogolo, mwinamwake, ndi kudzalengezera kwa sabata ya mawa, bwanji, izo zingakhale...Ife sitingakhoze kukhala anthu ochuluka kwambiri muno.

<sup>3</sup> Ndipo misonkhano ya mitundu iyi, ngati Mulungu alola, siyimalunjikitsidwa kwa...Iyo imalunjikitsidwira kwa Mpingo, kuti ipindulire Mpingo, kumene ife tikumverera kuti iyo ikufunikira kwambiri pa nthawiyi, konsekonse, ndi, aponso, kwa kumangiriza kwa Thupi la Khristu. Ndipo, tsopano izi, mu kuphunzitsa. Ine ndakhala ndiri ndi misonkhano ya machiritso kwa zaka eyiti, motsogozana; ndiyeno, kuphunzitsa, iko kukhala ngati chinachake chatsopano.

<sup>4</sup> Ndipo ine ndimaganiza, masana ano, pamene ine ndinatsegula Baibulo, nditakhala wotanganidwa kwambiri tsiku lonse. Ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndinawauza anthu kuti ine ndiphunzitsa pa *Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo*, mwinamwake, ngati Ambuye alola.” Ine ndinayamba kuwerenga, ndipo ndinadzangopeza zimenezo, mokondwera kwenikweni, pamene ine ndinayamba kuwerenga izo. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndikhoza kutenga zonsezo mu usiku umodzi, mu ora limodzi.”

<sup>5</sup> Chotero, ine sindikudziwa chimene Mzimu Woyera ungafune kuti ife tichite. Ife, ife sitimayesera kuti tikhazikitse chirichonse. Ndipo basi, “Ngati icho chingakhale chifuniro Chanu, Ambuye,” mwaona. Ndicho chopambana. Ndiyeno, ngati icho chingakhale chifuniro cha Ambuye, ine ndikufuna kuti ndiphunzitse usikuuno pa mibadwo ya mpingo, ndipo mawa usiku pa *Chilemba Cha Chirombo*, ndipo usiku wotsatirawo pa *Chisindikizo Cha Mulungu*, ndi zimenezo.

<sup>6</sup> Ndipo, kenako, Loweruka. Wanga, m'bale wathu, wosamalira pamalopa, amangondiwuza ine, lero; iye anati, “Ngati iwo akanakhala nayo Loweruka usiku ndi Lamlungu mmawa, kawirikawiri, pamene alendo abwera pakati pathu, bwanji, tchalitchi chimakhala chitadetsedwa kwambiri, ndi zina zotero.”

<sup>7</sup> Chotero iwo analingalira kuti tingokhala nayo Lachitatu, Lachinayi, ndi Lachisanu, ndi Lamlungu m'mawa, Lamlungu usiku. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, izo zingakhale zabwino mwangwiwo, momwe ine ndikudziwira.”

<sup>8</sup> Chotero ndiye ife tiyesetsa, ngati Ambuye alola, kudzakhala nayo Lachitatu, Lachinayi, Lachisanu, Lamlungu mmawa, ndi Lamlungu usiku. Ndipo, mwinamwake, Lamlungu usiku ife tikhoza kudzakhala ndi utumiki wa ubatizo, monga anthu akhala akufunsa kale za kubatizidwa. Ndipo chotero tsopano . . .

<sup>9</sup> Ndipo ife tiziyesetsa, usiku uliwonse, kuti tiziyamba mu nthawi yake, hafu-seveni. Ndipo tizitero, ine ndizifika pa nsanja ikamati eyiti koloko, ife tikuyenera kuti tizikhala titatuluka mkachisi ikamati hafu-naini, Ambuye akalola. Kuchitira kuti inu . . . Ine ndikudziwa kuti mumagwira ntchito, ndipo timalemekeza zimenezo.

<sup>10</sup> Ndipo tsopano Mauthenga aang'ono awa ochokera mu Bukhu la Chivumbulutso amalunjikidwa kupita kwa Mpingo. Ndipo ine ndikukhumba aliyense akanati azikumbukira izi, kuti iyo siyimalunjikidwa kupita ku chipembedzo cha aliyense, kapena cholinga china chirichonsecho; chokhacho basi, mwakupambana kwa kudziwa kwanga, ku kuwerenga ndi kufotokoza kwa Mawu a Mulungu. Mukuona? Sikuti ndi kukankhira kudutsa cholinga chodzikhonda chirichonse, kapena sikuti iwo amalunjikidwa kupita kwa aliyense, munthu aliyense, kapena tchalitchi cha aliyense, chipembedzo cha aliyense.

<sup>11</sup> Ndipo chifukwa chimene ine ndimakondera kuphunzitsa pa vumbulutso ili kuno ku kachisi, pokhala mpingo wanga womwe, bwanji, ine ndimangomverera ngati ndiri kwathu. Ndipo—ndipo ine basi, inu mukudziwa, ndimakhala ngati ndimazipatsa nkhosa zanga mtundu wa chakudya chimene ine ndimaganiza kuti izo zimachisowa, inu mukudziwa. Zina za- . . .

<sup>12</sup> Anthu, nthawizina amayenera kuthira mchere pang'ono pamene—a—alfalfa wachita nguwi, inu mukudziwa. Iye akhoza kuvulaza nkhosazo ngati simutero. Chotero, apo ndi apo, pamene mwinamwake alfalfa akachita nguwi pozungulira pa tchalitchi, ndi—ndipo kusamvetsana pang'ono kukabwera, chotero ine ndikuganiza kamchere pang'ono, kamakhala ngati, ndi kokometsera, kodi inu simukuganiza chomwecho? Iko kamakhala ngati kamawapangitsa iwo kuti asamadwale.

<sup>13</sup> Chotero tsopano ife tikupemphera kuti—kuti Mulungu atidalitsa ife mu kuyesetsa uku. Ndipo ndi angati...? Kungomverera, monga amuna ndi akazi, monga ife tiriri, ine ndikufuna kuti ndidzayang'ane mu zimenezo, mawa usiku, pa, “Kodi chilemba cha chirombo ndi chiyani?” Ziripo zochuluka za izo mu Baibulo. “Ndi ndani ali nacho icho? Ndipo ndani adzakhale nacho icho?”

<sup>14</sup> Ndipo kenako, chotsatira, padzabwera nthawi imene zimenezo ziti zidzakhale. Ndipo ine sindikudziwa, iyo ikhoza kukhala tsopano. Ife tidzayang'ana ndi kuwona, eya, kuti, padzakhala magulu awiri okha a anthu pa dziko lapansi, ndipo limodzi lidzayikidwa chilemba ndi mdierekezi, ndipo linalo chilemba cha Mulungu. Ndipo ine ndikuganiza, kuti ngati tikuyandikira ku nthawi imeneyo, zikanakhala bwino ngati tikanakamawunguza pozungulira, kukafufuza kuti chinthu chimenecho ndi chiyani, chifukwa icho motsimikizika sikuti chidzabwera kokha ngati chinthu chinachake chachikulu chopambana. Baibulo linati icho chidzazembera mophweka kwambiri, mwakuti, “Icho chikanadzanyenga osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka.” Chotero ife tidzayesetsa, ngati Mulungu alola, kuti tidzayang'ane kudutsa mu izo, mawa usiku. Tsopano, ndizo basi mwakupambana kwanga. . .

<sup>15</sup> Tsopano, mudzabwere ndi Baibulo lanu, ndi pensulo yanu ndi pepala, ndipo mungadzafune kumalemba Malemba. Ndipo, inu simukuganiza kuti zimenezo ndi zolondola ndendende, mudzandilembere ine kolemba kakang'ono ndi kudzakayika iko kwa usiku wotsatira.

<sup>16</sup> Ine ndikukumbukira nditakhala chaka ndi miyezi sikisi mu Bukhu ili la Chivumbulutso, mu—mu kachisi kuno. Ndi zimene ine ndimakonda, ndi—ndikamaphunzitsa. Ine ndimangokonda kuphunzitsa. Oh, mai! Ine—ine—ine—ine ndikuganiza kuti izo nzodabwitsa. Izo zimapereka maziko, ndi kuwukhazikitsa mpingo.

<sup>17</sup> Ndipo, mu kulalikira, tsopano, pali anthu ena amene ali alaliki. Iwo amakhoza kuwatenga Mawu, ndi kudzoza, ndi kuwazungulitsa Iwo kunja uko pamalopo. Kumeneko ndi kuthirira Mbewu zimene mphunzitsi waphunzitsa. Mukuona? Tsopano, inu mumayenera kuyika Mbewu ina mmenemo, poyamba, ndipo kenako nkumaithirira Iyo. Ndipo kuthirirako kumachokera ku kulalikira kwa Mawu.

<sup>18</sup> Pali kusiyana kwakukulu, zedi pakati pa mphunzitsi ndi mlaliki. Mukuona? Ndi mpmatso ziwiri zosiyana za Mzimu, pamodzi, mpmatso ziwiri zosiyana. Ndipo ndikunena ine modzichepetsa, koma, ine ndiribe mpmatso ya ziwiri zonsezo.

<sup>19</sup> Koma yanga, monga mwa nthawizonse, ndi kupempherera odwala. Ndicho chimene Ambuye anandiitana ine kuti ndidzachite. Ndiyeno, mu nthawi ino, izo zimandipatsa

kumasuka kwa malingaliro anga, kuti ndikuphunzitsa chinachake chosiyana, osakhala ndi misonkhano ya machiritso Auzimu; basi—kumangophunzitsa Mawu. Ndipo, oh, ife timagwirizana bwino kwambiri kuno. Ife...Ine ndikukumbukira, inu mwapirira nane ine kwa nthawi yaitali, pafupifupi zaka thweloфу kuzungulira kuno, pa izi.

<sup>20</sup> Ndipo ine ndinkakonda kunena ndi...Osati kutanthauza izo ngati nthabwala, koma, kuphunzitsa kumakhala kwaukali kwambiri, Ine ndinati, “Izo zimakhala ngati munthu akupita pa tebulo ndipo akudya nsima ndi nyemba.” Tsopano, izo zimakhala zabwino kwa iwe, koma iwe umatopa nazo pang’ono, apo ndi apo, umayenera kukhala ndi chinachake pambali pake, ayisikrimu wina ndi keke, kamodzi panthawi, kulola kuti zikhale ngati zakudya zamagulu. Koma zabwino zakachitidwe-kachikalezo zimakusunga iwe bwino, ndipo, bolako, zimakupatsa iwe poyambira pena.

<sup>21</sup> Tsopano, mu izi, ndi mwa chikhulupiro changa chodzichepetsa kuti ife tikukhala mmasiku otsekera a mbiriyakale ya dziko lapansi. Ine ndikufuna kuti ndizifotokoze zimenezo momveka bwino kwenikweni. Tsopano, ine ndikhoza kulakwitsa. Ine sindikudziwa. Palibe wina aliyense akudziwa. Yesu anati, “Ngakhale Angelo a Kumwamba sangadziwe.” Iye sankadziwa, Iyemwini. Iye anati, “Izo ndi za Atate okha, ndi Mmodzi yekhayo Amene akudziwa.” Koma ndi zotsimikizika ndi zovomerezeka kuti Iye akubwera. Ndipo ine basi sindikutha kuwona china chirichonse chimene chatsalira koma ku... Kudza kwa Ambuye.

<sup>22</sup> Pamene, ine ndiyang’ana ndi kuwona, fuko lasweka. Ndikuwona ndale zasweka. Ndikuwona manyumba asweka. Ndikuwona tchalitchi chasweka. Ine...Palibe china chirichonse chabe chimene chingakhoze kukonza zimenezo, koma Mulungu, ndizo zonse, chifukwa iwo alibe china chirichonse. Makhaliuwe a fuko asweka. Ndipo zipani zandale zasweka; kumene ife tinkadalira kwambiri mu ndale zathu; izo zasweka.

<sup>23</sup> Ndipo munthu wina wamkulu mu England, osati kale litali, anati, “Chabwino, demokalase inali—inali kumangoyenda panyanja wopanda nangula.” Amene anati, “Idzafika nthawi imene azidzaima pa makatoni asopo, nkumapanga zisankho.” Chabwino, izo nzoona. Koma iye sanalingalire za Nyumba yake yomwe ya Malamulo, momwe iyo inali kuyenda pa nyanja wopanda nangula, nayonso. Iyo inaphwasuka, nayonso.

<sup>24</sup> Ndipo ufumu uliwonse wa dziko lino udzaphwasuka mzidutswa. Yesu Khristu adzakhala mfumu ndi kumalamulira. Chotero pali:

Ziyembekezo zanga sizinamangidwe pa  
chirichonse  
Kuposa Magazi a Yesu ndi chirungamo;

Paliponse kuzungulira moyo wanga  
 pakupereka njira,  
 Iye ndiye chiyembekezo changa chonse ndi  
 pokhalapo.

Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndayima;  
 Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

<sup>25</sup> Ndipo, oh, momwe ine ndikanakhumba tsopano kuti  
 tikuyamba msonkhano wophunzitsa wa pafupifupi miyezi  
 itatu, kuti inu mukhoze kulowa mu Bukhu la Chivumbulutso  
 ndi kulimangirizira ilo mkati ndi la Daniele, masomphenya  
 aakuluwo.

<sup>26</sup> Ndi angati amene atsalira, mu gulu lapang'ono muno,  
 amene anakakumbukira pamene ine ndinkakhala ndi chojambula  
 nditachipachika apa? Ine ndikudziwa M'bale Head analipo,  
 ndipo ife tinali ndi angapo a inu pano pamene ine ndinali ndi  
 chojambula chakale.

<sup>27</sup> Tsopano, Bukhu la Chivumbulutso, momwe Ilo  
 linapangidwira. Ndipo Daniele amalumikizana nalo Ilo.  
 Yesaya amalumikizana nalo Ilo. Chipangano Chakale chonse  
 chimalumikizana nalo Ilo. Ndipo Ilo ndi Bukhu la Vumbulutso la  
 Yesu Khristu. Mukuona? Bukhu la Vumbulutso la Yesu Khristu.

<sup>28</sup> Ndiyeno, mmenemo, muli Mipingo Isanu Ndi Iwiri, Miliri  
 Isanu Ndi Iwiri, Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri, Malipenga  
 Asanu Ndi Awiri. Tsopano, lipenga limaimirira nkondo;  
 chisindikizo, chinsinsi chi- . . . chikamafutukuka; ndipo mliri ndi  
 chimene chimatsatira nkondo iliyonse.

<sup>29</sup> Ndipo ndi thandizo la Mulungu, ndipo ndi bukhu la  
 mbiriyakale, ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti ife  
 tikukhala moyo pa Lipenga Lachisanu Ndi Chiwiri, kuti Mliri  
 Wachisanu Ndi Chiwiri, ndi Chisindikizo Chachisanu Ndi  
 Chiwiri kuti chitsegulidwe, ndi Mbale Yachisanu Ndi Chiwiri  
 kuti itsanuliridwe.

<sup>30</sup> Pamene lachisanu ndi chimodzi liwomba; ife tidzafika  
 pa zimenezo, mwinamwake, kusindikizako, Lachisanu usiku.  
 Pamene Nkhondo Yadziko Lonse Yoyamba, bwanji, a . . .  
 Lipenga Lachisanu Ndi Chimodzi lija linawomba molingana,  
 ndendende molingana ndi nthawi imene Mulungu anayankhula  
 za ilo. Ndendende, mwa jogarafe, kutsatira chisindikizo izo  
 zisanati. Ndipo pamene chinsinsi chinawululidwa mmenemo,  
 kwa ubatizo wa Mzimu Woyera; ndipo—ndipo anthu nthawi  
 imeneyo, momwe mpingo sunasunthire chokwezeka; ndipo iwo  
 amene ankasuntha anakana kuti ayende mu Kuwala, ndipo  
 anabwerera mmbuyo. Ndipo mliri unatsegulidwa pa nthawi  
 imeneyo, ndipo unatsanuliridwa padziko lapansi, umene unali  
 chimfine, umene unapha anthu onse monga iwo unachitira,  
 masauzande kuchulukitsa masauzande.

<sup>31</sup> Ndipo kenako kubwera chotsika kudzafika mu m'badwo wotsiriza uno, umene ife tirimo pano. Ndipo tangobwera ndi kudzamvetsera zimene Ambuye angati anene za izo, mu Mawu Ake. Tsopano, izo si zopanga zanga. Ine ndizingowerenga izo ngati nyuzipepala, kuchokera mu Mawu a Mulungu. Chotero, Ili ndi vumbulutso Lake lolunjika kupita kwa Mpingo, kupita kwa Mpingo; Vumbulutso la Yesu Khristu, kupita kwa Mpingo.

<sup>32</sup> Tsopano, ife tisanayankhule kwa Iye, kapena kuyankhula za zolemba Zake, tiyeni tiweramitse mitu yathu ndipo tiyankhule ndi Iye mphindi chabe mu mawu a pemphero.

<sup>33</sup> Atate athu a Kumwamba achifundo, pamene ife mwaulemu tikuweramitsira mitu yathu ku fumbi, kumene ife tinatengedwako ndipo tidzabwererako tsiku lina, ngati Inu mungachedwe. Ife tikuweramitsa modzichepetsa, kuti tipemphe kuti Inu mukhale pafupi nafe, usikuuno, kuti mutidalitse ife. Ine ndikhoza kufunyulirira mmbuyo masamba a Baibulo ili, koma palibe munthu amene angakhoze kutsegula Bukhulo kapena kumasula zisindikizo zake. Ndipo zinalembedwa Umu, "Iye amene adzachotsa kuchokera mwa Ili, adzachotsedwa, gawo lake, la Bukhu la Moyo; ndipo amene adzawonjezera kwa Ilo, miliri ya Mulungu idzatsanulidwira pa iye."

<sup>34</sup> Atate, pozindikira, monga amuna ndi akazi achivundi takhala pano usikuuno, tikudziwa kuti ndife anthu opita-ku-Muyaya. Mulungu, mulole Mzimu Woyera ubwere, Mlembi wa Baibulo ili, ndipo mudzatsegule masamba awa kwa ife. Ndipo mulole wantchito Wanu wodzichepetsa, wopanda pake alalikire monga munthu wakufa kwa anthu akufa, ngati kuti uwu ukhala msonkhano wotsiriza umene ine ndikanati ndidzakhale nawo konse mbali ino ya Muyaya, usiku wotsiriza umene ife tidzasonkhane konse limodzi. Ndipo mulole aliyense wa anthu wamba achite usikuuno ngati kuti uwu ndi ulaliki wawo wotsiriza umene ati adzawumve konse. Mulungu, muchotsepo kupusa konse. Mutipange ife owonamtima, podziwa kuti ife tidzayenera kudzayankha pa Chiweruzo cha Mulungu, tsiku lina. Ndipo kachitidwe kathu kwa Iye ndi Mawu Ake, tsopano, katsimikizira kopita kwathu Kwamuyaya.

<sup>35</sup> Chotero, Atate, ndi mitima yonjenjemera, ife tikubwera kwa Inu, ndi kudzakupemphani. Mulole Ambuye Yesu, mmawonekedwe a Mzimu Woyera, awatenge Mawu a Mulungu, usikuuno, ndi kuwapereka Iwo kwa mtima uliwonse, monga ife tikuwafunira. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

<sup>36</sup> Izo zikhoza kuwoneka zachirendo pang'ono kwa ine, kwa mphindi pang'ono tsopano, poyesera kuti ndiyambe kutsegula phunziro loti ndiphunzitse. Chifukwa, izo nthawizonse zakhala ziri pa machiritso Auzimu kwa zaka zingapo zapitazi, ndiyeno,

kapena, ndiye, osati pa uneneri, mwanjira iliyonse, ndipo kenako—ndipo kenako nkudzapita mu mzere wa pemphero.

<sup>37</sup> Koma tsopano, usikuuno, ife tikufuna kuti titenge maziko a Bukhu limene ife tikumupempha Mulungu kuti atitsegulire ife, limenelo ndi Bukhu la Chivumbulutso cha Yesu Khristu.

<sup>38</sup> Bukhu ili linalembedwa pafupifupi A.D. 96, malingana ndi alembi, ndipo anali Yohane wokonedwa.

<sup>39</sup> Ndipo iye anali ndi masomphenya awa pa chisumbu cha Patmo, chisumbu mu Nyanja ya Aegean, pafupifupi mamailosi fifitini, kapena chinachake, kuzungulira icho, mozungulira, malo amiyala kwenikweni odzaza njoka, ndi zina zotero, kumene fuko la Chiroma linkawagwiritsa ntchito ngati Alcatraz, monga momwe ife tingakhalire nazo lero, malo osungirako zigawenga zimene boma silikanatha kuzisamalira.

<sup>40</sup> Ndipo Bukhu ili linalembedwa ndi wotsiriza wa atumwi a Ambuye wathu Yesu Khristu, zimakhulupiridwa kuti anali wokonedwa amene ankatsamira pa chifuwa Chake chitachitika chiukitsiro; ndipo Iye anati, “Kuli chiyani kwa inu ngati iye atachedwa kufikira Ine nditadza?” Yohane anafa, ndi ukalamba. Aliyense wa ofera anasindikiza umboni wawo ndi magazi awo omwe.

<sup>41</sup> Yohane, tsogolo lake linayenda motere: Iye anagwidwa, ndipo anabwatitsidwa mu m’phika wa mafuta kwa maora twente-foro, mafuta obwata otentha, ndipo popanda chilema chirichonse kubwera kwa iye. Ndipo anakamuika iye pa chisumbu, pongomuganizira, kuti anali mfiti, “Iye anawalodza mafutawo kuti asamuwotche iye,” iwo amatero. Zoono, iyo inali mphamvu ya Mulungu, imeneyo. Inu simungathe kuwubwatitsa Mzimu Woyera kuti utuluke mwa munthu. Bwanji! Chotero iwo anayesera kuti awubwatitse Iwo kuti utuluke mwa iye, koma Mulungu sakanaloleza izo. Ndipo Iye anali ndi ntchito yoti iye ayichite. Ndipo kufikira Mulungu atathana ndi munthu Wake, palibe chinthu mdziko chimene chingamuvutitse iye. Ndizo zonse.

<sup>42</sup> Tsopano, Yohane pokhala wokalamba, iye..iwo amauzidwa ndi azambiriyakale, kuti iye ankabweretsedwa ku—ku tchalitchi, kuti akalalikire. Ndipo anali wokalamba kwambiri, chinthu chokhacho chimene iye ankanena, chinali, “Ana aang’ono, muzikondana wina ndi mzake.”

<sup>43</sup> Ine ndikukuuzani inu, icho ndi chinthu chabwino kwambiri kuti ulalikirepo. “Ana aang’ono, muzikondana wina ndi mzake.” Pamene ine ndikukulamba, mu utumiki tsopano, ndipo wanga. . . pafupifupi mu chaka changa cha twente-wani. Ine ndimaganzira, nthawi zonse pamene ine ndikupita, kuti izi. . . Mochuluka pamene ine ndiganizira za Ambuye Yesu, ndi mochuluka pamene ine ndimayamba kupeza kuti ndi chikondi chimene chimaphimba chinthu chonsecho. “Chikondi

cha Mulungu, chitaphimba mokwanira mu mtima mwathu ndi Mzimu Woyera.”

<sup>44</sup> Tsopano ife tingowerenga ndime zingapo apa, kuti tikhale . . . tiyambepo, ndipo kenako ife tilowa mu kuphunzitsa kwa mpingo. Ndipo kenako tiyesera kuti tizifikitse izo pa malo, ngati Mulungu alola, mu nthawi yochulukira ino imene ine ndiri nayo, kuti tizifikitse izo kumene ife tingathe kufikako kumene ife tingathe kukatenga, *Chilemba Cha Chirombo*, za mawa usiku.

<sup>45</sup> Tsopano, izi ndi za kwa mpingo. Tsopano, ine ndiyesera kutenga, mwinamwake, mpingo wa Efeso, mpingo woyamba, ndi mpingo wotsiriza umene ife tikukhalamo tsopano, mpingo wa Laodikaya tsopano.

*Vumbulutso la Yesu Khristu, limene Mulungu analipereka kwa iye, kuti awonetsere kwa antchito ake zinthu zimene zikuyenera kuchitika posachedwapa; ndipo anamtumiza mngelo wake ndipo anazizindikiritsa . . . anatomiza ndi kuzizindikiritsa izo kudzera mwa mngelo wake kwa wantchito wake Yohane:*

<sup>46</sup> Tsopano, Lemba likutipatsa ife poyambira apa. Ilo ndi, “Vumbulutso . . .” Kapena, mawu akuti *vumbulutso amatanthauza* “chinachake chimene chaululidwa.” “Vumbulutso la Yesu Khristu,” loperekedwa kwa Yohane. Ndipo mngelo anatomizidwa kuti akachitire umboni, kapena kukazindikiritsa za izo.

*Ndipo iye anachitira umboni mawu a Mulungu, ndi umboni wa Yesu Khristu, ndi wa zinthu zimene iye anaziwona.*

*Wodala ndi iye amene awerenga, . . .*

<sup>47</sup> Ndi angati amene angafune kukhala ndi mdalitso? Ndiye, muziwerenga Ilo. Mwaona, “iye amene awerenga.”

*Wodala ali iye amene awerenga, ndi iwo amene amvetsera mawu a ulosiwu, ndi kusunga zinthu zimenezo zimene zinalembedwa mmenemu: pakuti nthawi yayandikira.*

<sup>48</sup> Mwa kuyankhula kwina, osati nthawi inayandikira *pamenepo*, koma, “Nthawi yayandikira, pamene iwo awawona Mawu awa akutsirizidwa, pamene Vumbulutso lathunthu.”

<sup>49</sup> Pamene Mulungu anayamba, ngati wojambula akujambula chithunzi cha chinachake, Iye akuyamba kudzazitsa magawo Ake. Inu mukhoza kuyamba kuchiwona icho chikuwumbika. Ndipo pamene inu mukuyambira koyambira kwa Bukhu la Chivumbulutso, inu mukumuwona Yesu Khristu akuyamba kubwera mu chithunzicho. Ndipo kumapeto kwa Ilo, inu mukumuwona Iye wathunthu, atakhala ndi Mpingo Wake,



waulemelo; masiku onse a tchimo ndi mavuto ndi mayesero atha, ndipo Khristu wakhala ndi Mpingo Wake, mu Miyamba yopambana mmwamba.

<sup>50</sup> Chabwino, ndime ya 4. Mvetserani. “Yohane kwa mipingo . . .” Tsopano, uyu ndi Yohane akuyankhula. Poyamba, anali Mulungu akupereka malonje Vumbulutso la Yesu Khristu. Kachiwiri:

*Yohane kwa . . . mipingo imene ili mu Asiya: Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, zochokera kwa iye amene ali, ndi amene anali, ndi amene ali nkudza; ndi kuchokera kwa Mizimu isanu ndi iwiri imene ili pamaso pa Mulungu;*

<sup>51</sup> Oh, ngati ife tikadangokhala ndi bolodi lakuda pano tsopano, kuti tijambule, pang’ono, mwaona, “Mizimu isanu ndi iwiri imene ili pamaso pa Mulungu.”

<sup>52</sup> Tsopano, kuti tisunge kanthawi pang’ono, ndipo kukhulupirira kuti ine . . . podziwa kuti sindingabwereze molakwika chirichonse, pachabe mdzikoli. Ndipo ngati inu mukaikira pang’ono za izo, mulembe zimenezo ndipo kenako mudzandifunse ine, ndipo ine ndidzakupatsani inu Lemba la izo. Ndipo tsopano monga ife tikuyenera kufulumira kuti tilowe mu izi, tapanikizika kwambiri chifukwa cha nthawi.

<sup>53</sup> Tsopano, “Mizimu isanu ndi iwiri imene ili pamaso pa Mulungu.” Mizimu isanu ndi iwiri iyi inkaimiridwa ngati Mizimu isanu ndi iwiri imene ikanati idzatumizidwe ku Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo, “Mizimu isanu ndi iwiri pamaso pa Mulungu.” Ife tikhoza kukatenga kuchokera ku Chipangano Chakale, ndi kukatenga mmenemo, ngati ife tingakhale ndi nthawi.

*Ndipo kuchokera kwa Yesu Khristu, amene ali mboni yokhulupirika, ndi woyamba kubadwa wa akufa, ndi kalonga wa mafumu a dziko lapansi. Kwa iye amene anatikonda ife, ndipo anatisambitsa ife . . .*

<sup>54</sup> Mai, tangomuyang’anani Yohane atamangika yense pamene, pamene iye anayang’ana. Iye akungoyamba kuyankhula. Iye anati:

*. . . -kwa iye amene anatikonda ife, ndipo anatisuka ife ku machimo athu ndi mwazi wake womwe,*

*Ndipo watipanga ife kukhala mafumu ndi ansembe kwa Mulungu . . . Atate wake; kwa iye kukhale ulemelo ndi mphamvu kwa nthawi za nthawi. Amen.*

<sup>55</sup> “Watipanga ife kukhala ansembe ndi mafumu kwa Mulungu.” “Ife” ndi zambiri. Osati “wandipanga ine kukhala wansembe ndi ka mfumu;” koma, “watipanga ife,” Mpingo.

<sup>56</sup> Tsopano, iye akuyankhula kwa mipingo isanu ndi iwiri iyi, pakuti iyo ndi Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo.

57 Tsopano, iye anati, “Mphamvu ndi ulemelero, ndipo zikhale kwa Iye kwa nthawi za nthawi.”

58 “Watipanga ife kukhala ansembe.” Kodi munayamba mwadziwapo chimene wansembe ali, chimene udindo wake uli? Wansembe ndi wakuti azipereka nsembe, kuti azipembedzera. Ndipo mu Ahebri, Ilo linanena kuti ife, Mpingo, ndife unsembe wachifumu, “Unsembe wachifumu, fuko loyera, anthu achilendo.” Mukuona? “Fuko loyera, anthu achilendo, unsembe wachifumu.” “Kupereka,” ndi izi apa tsopano: “kupereka nsembe zauzimu,” mwamuna ndi mkazi aliyense amene amabwera kwa Mulungu amalowa mu chophimba.

59 Mu Chipangano Chakale, mumakhala kokha a... pamakhala chophimba chimene chimapachikidwa pakati pa malo oyera ndi Oyeretsesa. Aroni basi, yekha, amayenera kukalowa mmenemo, kamodzi pa chaka. Koma munthu aliyense amene amadzakhala wansembe, amakhoza kukalumako, kapena kukalawa mana apachiyambi amene Mose ndi Aroni anawatola tsiku loyamba limene mana anayamba kugwa kuchokera kumwamba. Pamene iwo anawoloka mtsinje wa Yorodani. . .

60 Adaniwo anaphedwa, kumbuyo kwawo. Ndipo tsiku lotsatira iwo anatuluka, ndipo paliponse pansi, panali tokulumunya ting’ono ting’ono. Mulungu anavumbitsa ito kuchokera kumwamba. Iwo ankatitcha ito “mana,” ankakoma ngati uchi. Ndipo anthu ankangoyenera kuti atole okwanira kuti athe nawo tsiku limodzi limenelo. Ngati iwo awasunga iwo, iwo ankawonongeka.

61 Ndipo Mulungu anamuuza Mose ndi Aroni kuti apite ndi kukatola ma omeri-odzaza angapo a iwo, madengu aakulu, ndi kuwatengera iwo mu . . . pafupi ndi likasa, Malo Oyera.

62 Ndipo pamenepo, kuti, nthawi iliyonse kakadutsa kam’badwo kameneko, kuti kam’badwo kalikonse kotsatira iko, utali wa mmene unsembe wa chi Levi umenewo ungakhalire, ine ndikuganiza, kuti munthu aliyense amene anali woyenera kukhala wansembe, pamene iye adzozedwa kukhala wansembe, iye amakhala ndi ufulu wangwiwo kuti azilandira mana apachiyambi odzaza nkamwa. Taganizani za zimenezo. Ndi mwayi wotani umene amunawo ankaganiza kuti akhala nawo, pamene mwamuna adziwa kuti iye akubwera mu unsembe! Iye anali woti azitenga a—a chophikidwa chazimucho chodzaza nkamwa, chotakasidwa mwauzimu, chakudya chazimu chimene chimabwera kuchokera kwa Mulungu Kumwamba, chimene chinali chitasungidwa mwauzimu.

63 Utumiki wonsewo ndi chazimu. Anthu anganene bwanji kuti iwo ndi Akhristu, ndipo nkumakana chazimu? Ine sindikudziwa momwe iwo amachitira izo, inemwini. Penyani. Koma, chazimucho! Iye amameza chazimu, mwamsanga pamene iye akhala wansembe.

64 Ndi choyimira chokongola bwanji cha pano, kuti munthu aliyense . . . Masiku amenewo, iwo ankayenera kuti abadwire mu m’banja linalake, la Mlevi, iwo asanakhale wansembe, koma tsopano ndi “aliyense amene afuna, muloleni iye adze.” Mukuona? Ndipo mwamsanga pamene iwo abwera, chonchobe, iwo ayenera . . . Kubadwa kumaganiziridwa mmenemo, aponso. “Iwe umayenera kubadwanso mwatsopano.” Ndipo mwamuna aliyense kapena mkazi yemwe wabadwa mwatsopano, mwa Mzimu wa Mulungu, amakhala nawo ufulu wa (tsiku lino), mana. Mana awa ndi Mzimu Woyera.

65 Pamene Petro . . . atatuluka mu chisokonezo chachikulu, ndipo mantha anali atawachokera iwo, ndipo Ambuye anali kuwadalitsa iwo, ndipo Mzimu Woyera unagwa pa Tsiku la Pentekoste. Iwo anapita kunja mu msewu ndipo anayamba kufuula, ndi kumachita ngati anthu openga, mpaka kuti anthu onse ankaganiza kuti iwo aledzera. “Kumati, ndikudabwa kuti tichita nazo chiyani zimenezi?” Aliyense mu- . . . Ngakhale dziko lachipembedzo, pamenepo, linaganiza kuti anthu amenewo anali ataledzera.

66 Ndipo mvetserani, mzanga wa Chikatolika, namwali Maria wodala anali ndi iwo. Ndipo ngati iye sakanatha kukafika Kumwamba mpaka iye atakwera pamwamba apo ndi kukalawa Chinachake chimene chinamupangitsa iye kuchita ngati mkazi woledzera, inu mudzakafikako bwanji kumeneko ndi chirichonse chochepera kuposa icho? Koma iye analandira Chinachake. “Handiredede ndi twente, limodzi ndi akazi, Mariya wa Magadala ndi iwo,” ndipo anapita kunja mu msewu, kumakachita ngati anthu oledzera, akudzandima.

67 Mpaka weniweniwo (Ngati mungandikhululukire mayankhulidzewo.), mpingo wapamwamba wa tsiku limenelo unati, “Tayang’anani pa iwo! Zimenezo zikusonyeza chimene iwo ali. Iwo onse akhuta vinyo watsopano.”

68 Ndicho chimene Icho chinali. Tsopano mvetserani, Petro anati (Kenako iwo anayamba kunena . . .), iye anati, “Inu amuna aku Yerusalemu, inu okhala mu Yudeya, mulole ichi chidziwike kwa inu, ndipo mvetserani mawu anga: Awa sikuti aledzera.” Tsopano, ine ndikuyankhula za mpingo wa Aefeso apa, tsopano. Mukuona? Mukuona? Chabwino, m’badwo wa mpingo woyamba. Iye anati, “Awa sanaledzere, monga inu mukuganizira; Ili ndi ora lachitatu la tsiku; mabala sanatsegule nkomwe. Motani . . . ? Chabwino, ili ndi ora lachitatu la tsiku.” Iye anati, “Koma *ichi* ndi *chija* chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoweli. Zinalembedwa mu Baibulo lanu lomwe. Mu Baibulo lanu lomwe, izi zinalembedwa, kuti chinthu ichi chidzachitika. Bwanji,” iye ananena, kuti, “inu mumayenera kudziwa izi, inu aphunzitsi.”

69 Chabwino, kodi izo zingakhale, basi monga—monga mpingo unabweretsedwa pansu pa chiwonetsero chimenecho, ndipo

chiwonetsero chomwecho chinalonjezedwera masiku otsiriza, kodi inu simungalozere mmbuyo ndi kuti, “Ichi ndi chimene chinanenedwa?” Mukuona? Ndi zimenezotu. Ndipo dziko lakunja silimadziwa kalikonse za izo; izo—izo ndi zopusa kwa iwo. Tsopano iwo anati. . .

<sup>70</sup> Iye anati, “Onani apa.”

Ndipo iwo anati, “Tsopano. . .” pamene iwo anamva ichi.

Iye anawauza iwo momwe iwo anamupachikira Yesu. Ndipo nthawi zonse. . .

<sup>71</sup> Inu mukhoza kukhululukidwa pomupachika Yesu. Inu mukhoza kukhululukidwa chifukwa cholitenga Dzina Lake pachabe. “Koma amene ayankhula motsutsana ndi Mzimu Woyera, sadzakhululukidwa konse, mdziko lino, kapena dziko liri nkudza.” Ife tiri mmasiku otsiriza, chotero muzikhala osamala. Muzyienda odzichepetsa. Muzikhala a mtima wosweka, wosimidwa; wodzichepetsa, wololera kuti Mzimu Woyera uzikutsogolerani inu. Amen. Chabwino. Oh, mai!

<sup>72</sup> Ndi awa apa, iwo onse ali pamwamba apo, basi anthuwo akuchita ngati. . .Iwo anali amantha, maora angapo zisanachitike; atadzitsekera mchipinda chapamwamba. Koma pamene Mzimu Woyera unabwera pa iwo ndi kuzadzaza mitima yawo, anaturuka panja mmisewu! Ine sindikuganiza kuti iwo anali. . .Iwo samachita zinthu zimene zinali zoyipa. Iwo anali ali kunja uko akusangalala ndi kumutamanda Mulungu, mwa—mwanjira yakuti panali kuwonetseredwa. Sikuti iwo anali kunja uko akukangana wina ndi mzake tsopano, kaya iwo anali Amethodisti kapena Abaptisti, iwo anali, kapena kaya iwo anali Afarisi kapena Asaduki. Iwo anali kunja uko akusangalala chifukwa chakuti iwo anali atakulawa Kumwamba mmiyoyo yawo. Mulungu anali atawapatsa iwo mana auzimu.

<sup>73</sup> Tsopano, pamene Mulungu amatsanulira mana kumeneko mwathupi, ndipo iwo ankasungikabe nthawi yonse imene iwo anali paulendo; choimira chokongola. Ndipo tsiku limene iwo anakalowa mdziko lonjezedwa, mana anasiya.

Ndipo pa Tsiku la Pentekoste, chinthu chomwecho. . .

<sup>74</sup> Tayang’anani pa Pentekoste, kwa Mose. Iwo anayang’ana mmbuyo ndipo anawona kuti mdaniyo wafa. Miriamu anatenga nkhotcho, anayamba kuiyimba iyo, ndi kumafuula, ndi kumavina, ndi kumathamanga ku gombe. Akazi anamutsatira iye, akuchita chinthu chomwe chomwecho. Ndipo Mose anakweza mmwamba manja ake, ndipo anayimba mu Mzimu.

<sup>75</sup> Pa Pentekoste, akazi anatuluka, akuzandima, ndipo akulumpha, ndi kumavina, ndi kumapitirira. Petro anaimirira pakati pawo, ndipo anati, “Inu amuna aku Yudeya, ndi inu okhala mu Yerusalemu, mulole ichi chidziwike kwa inu, ndipo mvetserani mawu anga: Pakuti awa sanaledzere, monga inu

mukuganizira, pakuti ndi ora lachitatu la tsiku. Ichi ndi chija chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoweli; 'Izo zidzachitika mmasiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse: ana anu aamuna ndi aakazi adzanenera: pa adzakazi Anga ndi antchito Ine ndidzatsanulira cha Mzimu Wanga; ndipo iwo adzanenera: Ndipo Ine ndidzawonetsera zodabwitsa mmiyamba kumwamba, ndi pa dziko lapansi mmusi; mizati ya moto, ndi nthunzi, ndi utsi: Ndipo izo zidzachitika, tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye lisanadze, kuti yense amene adzaitanira pa Dzina la Ambuye adzapulumutsidwa.'" Mopitirira ndi mopitirira iye anapita, akulalikira.

<sup>76</sup> Ndipo pamene iwo anamva ichi, iwo anamvetsera. Anati, "Tamuwonani munthu ameneyo! Kodi iye wawapeza kuti maphunziro awa?" Ena a iwo anati, "Iye samatha nkomwe kulemba dzina lake." Baibulo linati, "Iye anali mbuli ndi munthu wosaphunzira. Kodi akuchokera ku sukulu yake iti? Palibe. Chabwino, kodi izi zatheka bwanji? Kodi izi zachitika bwanji?" Iwo anamvetsera, anati, "Chabwino, titi, munthu ameneyo ndithudi akuwerenga mobwereza Lemba. Ndipo ife sitinayambe tawamvapo Iwo monga chomwecho." Mukuona?

<sup>77</sup> Iye anati, "Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ana anu, kwa iwo amene ali kutali, ndi onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana." Mwakuyankhula kwina, "Mdalitso wa mana uwu umene wagwa apa, monga anachitira mana kumbuyo uko, ukhala wa kam'badwo kano, kam'badwo kotsatira, kam'badwo kotsatira, ku Jeffersonville, Indiana, ndi kumadera akutali a dziko lapansi."

<sup>78</sup> Ndipo Mzimu Woyera womwewo umene unagwa *pamenepo*, ukugwa *tsopano*; zotsatira zomwezo, chinthu chomwecho, anthu omwewo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Zangwiro basi!

<sup>79</sup> Zindikirani, "Ine ndidzapereka kwa iye; iye amene alakika, Ine ndidzamupatsa iye Mkate wa Moyo." Iye ananena zimenezo kwa umodzi wa mipingo. "Ndipo iye sadzamvanso ludzu, ngakhalenso kumva njala. Iye sadzamvanso ludzu." Ngati mwamuna kamodzi kokha (Ndi ichi apa; mumangitse jekete mothinita.), ngati mwamuna kapena mkazi alandira moonadi Mzimu Woyera kamodzi, inu simudzakhoza konse kumusunthanso iye. Iye amadziwa pamene iye ali. Inu mukhoza kubwera ndi timalingaliro ndi chirichonse. Iye adzayenda molunjika kudutsa zimenezo. "Iye sadzamvanso ludzu." Iye amadziwa ndendende basi Yemwe Mlengi wake ali; sadzasokonezeka konse. Sizingamusautse iye; iye amasunthabe chitsogolo.

<sup>80</sup> “Ine ndidzapereka kwa iye za Mkate wa Moyo, ndipo sadzamvanso njala kenanso, komanso sadzamva ludzu nkomwe.” Mukuona? “Ndipo Mtengo umene uli pakati pa paradiso wa Mulungu, ndipo iye adzadyako, mwaona, Mtengowo.” Chimene, Mtengowo unali Khristu Yesu. Mukuona? Ndipo Khristu Yesu, pokhala wakufa ndipo anabweranso mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, chotero Iye ali pano, ndipo ndi mana amene akudyedwa mu Mpingo.

Zindikirani, taonani, kuti, ndime ya 6.

*Ndipo iye watipanga ife ansembe ndi mafumu kwa Mulungu. . .*

<sup>81</sup> “Unsembe wauzimu; fuko lachifumu; chopereka chauzimu.” Ndi chiyani tsopano chimenecho? “Nsembe zauzimu, ndiko kuti,” kubwereza Lemba, “ndiko kuti, zipatso za milomo yathu kupereka matamando ku Dzina Lake.” Tsopano, mtundu wanji wa chiyani? “Nsembe yauzimu.”

<sup>82</sup> Tsopano, tsopano ife tikhoza kuyamba pomwe apa; zindikirani, malo abwino oyambirapo.

<sup>83</sup> Pamene chisokonezo pang’ono chibwera mu tchalitchi, inu simumathamangira ku mbali imodzi ndi kukanyogodola tsopano. Ngati inu mutero, inu ndithudi si wansembe. Mwaona, iwe umakapemphera mobowoleza. “Nsembe yauzimu, zipatso za milomo yathu kupereka matamando kwa Dzina Lake.” Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>84</sup> “Chabwino,” inu mukuti, “Ine sindikumverera basi kuti ndipite ku tchalitchi.” Koma ndiwe wansembe. Ndi ntchito yako. Iwe ukuyenera kukakhala kumeneko.

<sup>85</sup> “Chabwino, ine sindikumverera ngati nditenge gawo mu msonkhano.” Ndiwe wansembe, “kupanga nsembe, nsembe yauzimu.” Osati kumupatsa winawake zongolandira, monga iwo amazitcha izo lero; izo zonse nzabwino, ine ndiribe kanthu kotsutsa izo. Osati kupita kukamutenga winawake kuti abwere ku tchalitchi; izo zonse nzabwino, ine ndiribe kanthu kotsutsa izo. Koma, ndi *inu, inu* mukupereka nsembe yauzimu, “zipatso za milomo *yanu* zikulemekeza Dzina Lake.”

<sup>86</sup> Pamene inu muwona nthawi ikubwera imene aliyense akuchitira mwano ndi kumanena zinthu izi, ndi kumachita zinthu molakwitsa, inu mumachita chiyani, kuchokapo? Inu mukuyenera kuyima pamenepo ndi nsembe yauzimu, kunena kuti, “Magazi a Yesu Khristu amatsuka ku tchimo lonse,’ amandipanga ine kukhala cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu.”

“Ndiwe munthu, wopenga!”

<sup>87</sup> “Malingana ndi zimene inu mukunena. Izo ziri bwino. Koma kwa ine, ‘Ndi mphamvu ya Mulungu yaku chipulumutso.’ Ine ndikukhulupirira Zimenezo.” Mukuona?

88 Tsopano, iwo amati, “Inu mumakhulupirira mu machiritso Auzimu?”

“Oh, uh, ine sindikudziwa, inu kulibwino muwafunse abusa athu.”

89 Kodi *inu* mukuganiza chiyani za izo? Ndinu wansembe tsopano. Ndinu munthuyo. Nenani, “Inde, bwana. Ine ndimakhulupirira Izo, chifukwa Mawu a Mulungu amati Izo ziri chomwecho.”

“Inu mumakhulupirira mu ubatizo wa Mzimu Woyera?”

“Inde, bwana.”

“Inu mukudziwa bwanji?”

“Ine ndawulandira Iwo.” Mokwanira ndithudi. Mdalitso wauzimu! Mzimu Woyera umene unagwa pa atumwi, Mzimu Woyera womwewo ukugwa tsopano.

90 Inu mukuti, “Wa atumwi okha.” Ife tizikhazikitsa zimenezo nkanthawi pang’ono, tiwone ngati izo ndi choncho kapena ayi.

91 Chabwino, “Unsembe wauzimu, kupereka nsembe zauzimu.”

Tsopano, tsopano ndime ya 8, kapena, ya 7.

*Taonani, iye akudza mmitambo; . . .*

92 Tsopano, ndiroleni ine ndiyime apa mphindi yokha. “Mitambo,” sizikutanthauza kuti Iye akubwera pa mtambo waukulu wa bingu monga Amayi, adalitse mtima wawo, iwo akhala pano penapake.

93 Pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, iwo anakonda kukhala ndi kumandiuza ine, ankati, “Iye akubwera atakwera. Mtambo wawukulu kwambiri udzawuka tsiku lina, ndipo Mulungu adzabwera.”

94 Ndipo, tsopano, *mtambo* umene Iye akubweramo (Ngati ife tikanangokhala ndi nthawi yoti tizitengere zonsezi mmbuyo, ndi kupeza maziko enieni a chinthu chonsecho.), tsopano, *mtambo* umene Iye akubweramo, si mtambo ngati mtambo wa bingu, koma, iwo ndi “mtambo wa ulemelero,” Iye akubwera mmenemo. Mukuona? Mukuona?

95 Tsopano, pamene Yesu anaphimbidwa ndi Mulungu, pa Phiri la Chiwalitsiro, “mitambo inamuphimba Iye ndi chovala Chake.” Mukuona?

96 Ndipo pamene Eliya anadzatsika, mtambo unatsika ndipo unamulandira iye mmwamba. Osati a—osati Lawi la Moto, osati. . . Ine ndikutanthauza, osati mtambo wa bingu, koma, “mtambo wa ulemelero.”

97 Kukhalapo Kwake, kwakukulu kwa ulemelero kudzakantha dziko lapansi. “Iye akubwera mmitambo.” Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. “Mitambo,” padzakhala funde pambuyo pa funde, la

ulemelero Wake, lidzabwera padziko lapansi, ndipo chiukitsiro cha oyera chidzabwera. Pamene Mzimu Woyera wodala uwo umene umakhala mmitima yawo, ndipo iwo anafa, ndi mitembo yawo itagona pamenepo, ndi madontho a misozi pa masaya awo, ndi zinthu monga choncho, ndipo iwo nkuikidwa kunja kuno mmanda. Funde lalikulu la Mzimu womwewo, ndi “whuushi,” funde pambuyo pa funde.

<sup>98</sup> “Iye amene anali wotsiriza adzakhala woyamba, ndipo iye amene anali woyamba adzakhala wotsiriza.” Zingakhale bwanji mwanjira imeneyo? Ndiro dongosolo la chiukitsiro. Ine sindidzamujiwa aliyense wa kam’badwo ka mmbuyo mwa ine, kapena kam’badwo ka patsogolo pa ine. Ndidzawadziwa iwo amu kam’badwo *kano*. Ndipo kam’badwo kalikonse kadzabwera, mopambana, chimodzimodzi monga iwo unapitira pansi. “Iwo amene anali otsiriza adzakhala oyamba.” Ndithudi, izo zikuyenera kutero. Mukuona? Ine ndidzawadziwa anthu anga. Munthu wotsatira, adadi anga, adzawadziwa anthu awo; agogo awo, anthu awo; mpaka mmusi monga choncho.

<sup>99</sup> Funde pambuyo pa funde, pambuyo pa funde, pambuyo pa funde, ndipo oyera akuwuka kuchokera kulikonse. Kodi izo sizidzakhala zodabwitsa? Amen. Zimenezo zimawapangitsa anthu achikulire kudzimvanso achichepere. Inde. Tsopano zindikirani mwatcheru. Chabwino.

...akubwera mu—*mmitambo*; *ndipo diso lirilonse lidzamuwona iye*, (Ziribe kanthu kuti iwo anafa kalekale mmbuyo, iwo adzamuwonabe Iye.) *ndipo iwo nawonso amene anamupyozza iye: ndipo abale ake onse a dziko lapansi adzabuma chifukwa cha iye. Ngakhale chomwecho, Amen.*

<sup>100</sup> John ankangoyenera basi kuti afuule, “Amen.” Ndizo, “Zikhale chomwecho. Zisiyeni izo zikhale mwanjira imeneyo.”

*Ine ndi Alfa ndi Omega, . . .*

<sup>101</sup> Tsopano, *Alfa* ndi “A” mu zilembo za Chigriki. *Omega* ndi “Z” mu zilembo za Chigriki. Tsopano, mwa kuyankhula kwina, ngati izo zikanamasuliridwa lero, “Ndine A mpaka Z.” Tsopano, ndindani winanso ali pamenepo? “Ine ndine Woyamba; Ine ndine Wotsiriza. Ine ndi wochokera ku A mpaka Z.”

<sup>102</sup> Ndikanakonda ife tikanakhala ndi nthawi yolowa mu Umulungu wa Khristu, pakali pano, chimene chikanakhala choyenera kwambiri pa nthawi ino, Umulungu.

<sup>103</sup> Chotero, mmasiku amene anthu ambiri akuyesetsa kuti angomupanga Iye kukhala mphunzitsi, namatetule chabe, kapena mneneri wamba chabe. Iye anali Mulungu. Iye anali mwina Mulungu kapena wonyenga wamkulu amene dziko linayamba lakhalapo naye. Ngati Iye anali mneneri, magazi ake anali a munthu. Ngati Iye anali a—mphunzitsi, wophunzitsa, magazi ake anali a munthu.



<sup>104</sup> Iye anali Mulungu, ndipo Magazi Ake anali Auzimu. Mulungu Wamphamvuzonse anamuphimba namwali Mariya ndipo analenga khungu la Magazi mu chiberekero chake limene linabereka Mwana, Khristu Yesu. Ndipo Mulungu anatsika ndipo anadzakhala mu thupi limenelo, Mulungu (Emanuele), anasandulika thupi pakati pathu; kudzachotsa machimo.

<sup>105</sup> Pamene Mulungu anampanga munthu Wake woyamba, Iye anampanga iye mu chifanizo Chake Chomwe, amene anali munthu wauzimu, mu Genesis 1:26. Chabwino. Kenako panalibe munthu woti azilima mnthaka, Iye atatha kumupanga munthu, mwamuna ndi mkazi. Iye tifika mu zimenezo, pakapita kanthawi, pa “nyenyezi sevenizo.” Koma basi... Koma Iye anamupanga iye zonse ziwiri mwamuna ndi mkazi, kumbuyo uko pachiyambi, uko nkulondola, “mu chifanizo Chake Chomwe.” Ndipo Mulungu ndi Mzimu.

<sup>106</sup> Ndipo kenako, Genesis 2, kunalibe munthu woti azilima mnthaka, chotero Mulungu anamuika iye mu thupi; anamupanga munthu, osati mu chifanizo Chake, koma kuchokera ku fumbi la dziko lapansi (Ndiko kulondola.), anamupatsa iye dzanja ngati nyani, ndi phazi ngati chimbalangondo, kapena chirichonsecho; ine sindikudziwa, koma Iye anamupatsa iye zokhudzira zisanu kuti azilumikizana ndi nyumba yake ya padziko lapansi. Ndipo kenako munthu ameneyo anadzachimwa.

<sup>107</sup> Ndipo Mulungu anadzatsika ndipo anadzapangidwa munthu, kuti adzachotse tchimo la munthu (Ameni.), kuwombola.

*Ine ndi Alfa ndi Omega, . . .*

<sup>108</sup> Ine ndinayang’ana pa Iye cha apa mu Chivumbulutso mutu wa 4. Pamene Yohane anapotoloka kuti awone Liwu ili kachiwiri, limene linkayankhula kwa iye, “Iye anali atakhala pa Mpandowachifumu, ndipo utawaleza unali pamwamba pa mutu Wake.” Ndipo utawaleza uli ndi mitundu seveni yangwirowo, ndipo mitundu seveni yangwirowo iyi inkayumira Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Izo nzoona, kachiwiri. Ndipo icho chinali chiyani? Ndi ichi apa. M’bale, izi ndi zatsopano. Taonani, mitundu seveni yangwirowo, seveni, ndipo utawaleza umayimira pangano.

<sup>109</sup> Mulungu anamupatsa Nowa utawaleza, poyamba, ngati pangano. Ndipo zida zimenezo zikadali padziko lapansi, monga Mulungu analonjezera kale, ndipo pamene ivumba, ndipo Iye nkuwona utawalezawo. Iye amati, “Ine sindidzaliwononganso ilo ndi madzi kenanso.”

<sup>110</sup> Ndipo kenako iye anayang’ana pa Yesu, anali ndi mitundu seveni ya utawaleza pamwamba pa Iye; Iye anali mu ichi, chimene chinali pangano la Mulungu. Ndipo Iye anali atayima pakati pa, Zoyikapo Nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide. “Ndipo

Iye anali woti ukamamuyang'ana amawoneka ngati mwala wa yaspi ndi sardio.” Yaspi anali Rubeni, ndipo mwala wa sardio unali Benjamini; amenewo anali woyamba ndi wotsiriza wa mbadwa. Ameneyo “Alfa ndi Omega, Woyamba ndi Womaliza,” ndipo mitundu seveni ya utawaleza, Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo, pangano ndi Iye, mu Zoyikapo Nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri. Oh, ndi chithunzi chotani, ngati ife tingafike kwa icho pakapita kanthawi, mwinamwake, Ambuye akalola. Chabwino.

*. . . Alfa ndi Omega, woyamba ndi womaliza, atero  
Ambuye, amene ali, . . . amene anali, ndi amene ali  
nkudza, Wamphamvuzonse.*

<sup>111</sup> Ooh! Kodi Iye ndi ndani? Kodi vumbulutso ili ndi la chiyani? Yesu Khristu. Ndipo, apa, Iye si mneneri. Apa, Iye ndi Wamphamvuzonse, Mulungu akuwonetseredwa; Alfa, Omega. “Ndine kuyambira A mpaka Z. Ndine Iye Amene Anali, Amene Ali, ndipo Amene Adzabwera. Ine ndi Wamphamvuzonse.” Zikumveka bwino, sichoncho izo? Palibe mwayi wotsutsa pamenepo. “Ambuye, Amene Anali, Amene Ali, ndi Amene Adzabwera, Wamphamvuzonse.”

<sup>112</sup> Tsopano Yohane akuyankhula. Mvetserani.

*Ine Yohane, amenenso ndiri m'bale wanu, ndi  
wachifundo mu chisautso, ndi mu ufumu chipiriro cha  
Yesu Khristu, ndinali pa chisumbu chotchchedwa Patmo,  
chifukwa cha mawu a Mulungu, . . .*

<sup>113</sup> Titi, kodi inu mungalingalire munthu akuikidwa mmalo ngati amenewo, chifukwa cha Mawu a Mulungu? Inde.

*. . . chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi . . . umboni wa  
Yesu Khristu.*

<sup>114</sup> Iye anakaikidwa mndende kumeneko chifukwa cholalikira Mawu kwa anthu achipembedzo. Ndicho chimene Mawu amanena. Sichoncho izo? Iye anali kunja uko chifukwa cholalikira; anakaikidwa mndende, anachotsedwa ku tchalitchi, anamuchotsa ku gulu, anamuchotsa kwa dziko lonse. Amen. Koma iye sanachotsedwe kwa Iye Amene ankamukonda iye ndi kumusambitsa iye mu Magazi Ake Omwe. Iye anali ndi Kukhalapo Kwake, pa chisumbu chotchchedwa Patmo, “chifukwa cha Mawu a Mulungu.”

<sup>115</sup> Ine ndikudabwa ndi alaliki angati lero angapiteko? Amatsika mpaka iwo amapita kukachita chinachake chaching'ono—chinachake chaching'ono, chikasokonekera, ife timabalalika nazo kwambiri izo. Ndipo apa munthu uyu anali atawiritsidwa mmafuta kwa maora twente-foro, ndipo anakaponyedwa uko pa chisumbu cha Patmo, ndipo Ambuye anali akadali ndi iye.

116 Ine ndimangoikonda nyimbo yakale ija yomwe iwo ankakonda kuiyimba, “Ngati Yesu apita nane, ine ndidzapita kulikonse.” Ife timaiyimba iyo, koma ndikudabwa ngati ife timatanthauza iyo kwenikweni. Mwa kulingalira kwanga kowona, sizitenga nthawi yayitali mpaka inu mupatsidwa mwayi kuti mutsimikizire izo, chotero zikanakhala bwino kuti muzikhala otsimikiza kwenikweni. Muziyang’ana, nkumafufuza, nkuwona ngati chirichonse chiri bwinobwino basi.

117 Tsopano, basi bwanji, ndangoyamba kumene tsopano apa. Yohane akuyankha, ndipo iye anati iye anali “pa chisumbu cha Patmo, chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndi umboni.”

*Ine ndinali mu Mzimu . . . (Ine ndikuzikonda zimenezo.)*

*Ine ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye, . . .*

118 Akuyankhula za tsiku lina, tsopano; kwa azimzanga a Advent, chimene ife tikutsimikiza kuti tilowamo, pakapita kanthawi. Chabwino.

*. . . mu Mzimu pa tsiku la Ambuye, ndinalowa mu Mzimu, ndipo ine ndinamva kumbuyo kwanga liwu lalikulu, . . . la lipenga,*

119 Tiyeni tisasiye ziphiphiritso izi tsopano. Ife tikukhazikitsapo tsopano, kuti tidziwe zimene tikuzikamba pamene ine ndifika cha apa. Kuwona zimene titi tiyankhulepo, “Kodi ndi Ndani? Kodi Munthu uyu ndi ndani? Kodi Vumbulutso la Yesu Khristu ndi chiyani? Kodi Iye ndi ndani, mulimonse? Kodi Ilo linabwera bwanji? Kodi Ilo limatanthauza chiyani kwa ine?” Muone ngati Ilo limatanthauza chirichonse kwa inu, mwaona. “Muone chimene chikuchitika pamenepo, kwa ine.” Zindikirani.

*Ine ndinali mu Mzimu . . .*

120 Ziribe kanthu kaya ndinu woyera bwanji, kaya ndinu waumulungu bwanji, kaya ndinu mtumiki mochuluka bwanji kapena membala wamba, chirichonse chimene inu muli, inu simudzatha konse kufika kulikonse ndi Mulungu mpaka inu mutalowa mu Mzimu. Uko nkulondola. Ine sindikutanthauza kulowa mu kutengeka. Ine ndikutanthauza kulowa mu Mzimu. Mukuona? Mukuona? Mwaona, inu mumalowa mu zotengeka, kuchita chirichonse. Koma pamene inu mulowa mu Mzimu, inu mumawona zinthu. Uko nkulondola.

121 Ine ndikukhoza kumulingalira Eliya wakale, mneneri wakale, kumusi uko tsiku lija pamene—pamene a . . . pamene mwana wa Ahabu, iwo, anapanga mgwirizano ndi osakhulupirira ena, ndipo—ndipo Yehosafati anali ataphatikana ndi iwo. Ndipo iwo anapita uko mchipululu kwa masiku seveni, ndipo sanapeze namulondola aliyense. Kwa masiku seveni okha,

okwanira kuwasamalira iwo masiku seveni; sanafunsire kwa Ambuye; anangopita kumeneko, mulimonse.

<sup>122</sup> Kodi zimenezo siziri chimodzimodzi basi ndi anthu? “Oh, ine ndikukuuzani inu, imeneyo ndi ntchito yabwinoko. Ine ndingosiya tchalitchi *ichi* ndipo ndipita ku china *icho*.” Tsopano, inu kulibwino muzifunsira kwa Ambuye za icho, kufufuza chimene icho chiri.

<sup>123</sup> Anapita kunja uko ndipo anakapezako kuti iwo ali mu vuto. Madzi anatsekedwa. Ndiro limene liri vuto ndi matchalitchi lero, kumangoyendayenda nkumachita zinthu zambiri zimene inu simunafunsire kwa Ambuye za izo, ndipo thandizo lanu likudulidwa. Inu mukudabwa bwanji simukupeza madalitso amene munkapeza, ndi mphamvu ya Mulungu ikugwira ntchito pa inu, mwinamwake mpita wa thandizo wadulidwa. Inu mukudziwa, pamene inu mutulukapo, madzi. . .

<sup>124</sup> Ine ndimapita mchipululu nthawiya, kunja uko ku Arizona. Ndipo ine ndinawona kuti chitsamba chakale chaching’ono chirichonse mchipululu chimenecho ndi chokuvulaza; icho chimakumata iwe. Nthawi iliyonse ukachikhudza icho, icho chimakumata iwe. Chifukwa icho chiribe madzi okwanira oti asamalire icho, zisoso zimadzuka kuti zikatetezere.

<sup>125</sup> Iwe ukabwerera mmbuyo kuno, kapena uko mu Oregon kapena kwinakwake kumene kumavumba mvula nthawi zonse, ndipo chirichonse cha izo mtundu womwewo wa tchire wopanda zomata pa iwo. Mwaona, madzi amawafewetsa iwo.

<sup>126</sup> Ndipo ndiro limene liri vuto ndi tchalitchi. Pamene inu muwuma ndi kumangidwa maunyolo, ndi chirichonse, inu mumakhala ozizira kwambiri ndi ofunda ndi osayanjanitsika, inu simupeza mdalitso uliwonse wauzimu, zikatero mtima wanu wonse umadzazidwa ndipo umadzazidwa ndi ukali ndi mkwiyo, ndipo, aliyense, “Oh, ine ndidzamubwezera iye. Ine ndidzamubwezera iye. Ine ndisiya tchalitchicho.” Basi gulu la zomata zomwe zikukhala mchipululu. Uko nkulondola. Chimene inu mukusowa ndi Madzi ena abwino a Mzimu Woyera wakachitidwe-kachikale avumbire pa inu, afewetse mtima wouma wakale uwo. Amen.

<sup>127</sup> Ine sindiri—sindikuyesera kuti ndichite zisudzo. Ine ndikuyesetsa kuti ndifikitse izi kwa inu. M’bale, inu mudzapeza, ngati inu mudzatenga chilemba cha chirombo, pamene inu muti mudzakhale mutaima. Ndipo inu mwamtheradi mudzakhala wopanda thandizo ndi wopanda chiyembekezo pamene inu mudzatero. Palibe chikhululukiro kwa izo. Inu simungadzatuluke konse mu izo. Uko nkulondola. Inu mukhoza kuchita izo mwa kuphethira kwa diso lanu, pafupifupi, mwaona, chotero muzikhala osamalitsa. Tsopano ndi izi apa. Adzapereka kwa iye. . . Zindikirani, chipululu. . .

128 Ine ndinati, a—madzi, momwe madzi amasungira icho kukhala chofewa. Ndi chimene ife timachita lero, kulowa mu Mzimu. Yohane anati, “Ine ndinali mu Mzimu.”

129 Pamene Eliya kunja uko mchipululu, iwo anabwera kumeneko. Yehosafati anati, “Tiyeni tipite uko ndipo tikafunsire kwa mneneri.” Iwo anapita pamaso pa mneneriyo.

130 Chabwino, tsopano, iye anawukitsa ukali wake wachirungamo. Iye anayang’ana kwa munthu ameneyo, ndipo anati, “Bwanji osapita kwa mulungu wa amayi ako? Bwanji sukubwerera ku tchalitchi chako, chakale, chozizira, chofunda? Nchifukwa chiyani iwe wabwera kwa ine, pamene wakumana ndi vuto?” Icho sichinali chinthu chabwino kuchinena, koma amenewo ndi mawu ochuluka chabe kuti akatanthauze zimenezo. “Nchifukwa chiyani iwe wabwera kwa ine? Bwanji sunapite kwa mulungu wa amayi ako? Inu nonse muli ndi matchalitchi aakulu abwino awo, ndi ansebe onse odyetsedwa-bwino awo, ndi zina zotero, kumbuyo uko. Bwerera mmbuyo ndipo ukawafunse iwo za izo. Chifukwa chiyani iwe wabwera kuno kwa ine?” Psyii. Mai. Iye anakhala ngati anadzitukumula yense, ndithudi mokwanira, sichoncho iye? Iye anati, “Ndikanakhala kuti sindinalemkeze kukhalapo kwa munthu waumulungu uja, Yehosafati, ine sindikanakuyang’anani inu nkomwe.” Oh, mai, ndi chikhaliidwe chotani chimene mneneri ameneyo analowamo. Tsopano iye ali mu vuto la mtundu woterewo.

131 Iye anati, “Chabwino, ndibweretsere ine woyimba.” Anthu ena sakhulupirira mu nyimbo za mtchalitchi. Koma iye anati, “Ndibweretsere ine woyimba.” Ndipo pamene woyimbayo anayamba kuyimba nyimbo yakale yabwino, *Pafupi, Mulungu Wanga, Kwa Inu*; iliyonse imene mukufuna kuitcha iyo, ine sindikudziwa. Pamene woyimbayo anayamba kupemphera, Mzimu wa Mulungu unafika pa mneneriyo. Ndipo pamene Mzimu unafika pa iye, iye analowa mmasomphenya; anayamba kuwona zinthu.

132 Inu mukuyenera kutenga Mzimu wa Mulungu. Apo ayi, inu muziti, “Sindimamvetsa momwe anthu amakhoza kunenera, ‘Ameni.’” Mudzalowe mu Mzimu kamodzi. Uko nkulondola.

133 Ine sindimawona momwe iwo amaimirira ku masewero a mpira ndi kumamenyana ku nsana wina ndi mzake, ndi kumafuula ndi kumakuwa, ndi kumakokera zipewa pansu ndi kumapitirira. Zimawoneka ngati zopenga, kwa ine. “Chabwino,” inu mukuti, “sindiwe bwenzi labwino kwambiri la mpira.” Ine ndiri pafupifupi basi momwemo. . .

134 Nanga bwanji inu, ngati Mkhristu? Chabwino. Uko nkulondola. Inu mukuyenera kulowa mu Uzimu wa izo.

135 Umo ndi momwe zinkakhalira pamene inu munkakonda kupita kokavina. Ine sindikukhulupirira kuti inu mungapiteko

pakali pano. Ayi ndithu. Koma ngati inu—inu munkakonda kupitako, iwo amakaimbako nyimbo za gwedemula, ndi kumenya mabandi ndi kumamenya ng’oma, ndi kumachita mtundu uliwonse wa chinthu chimene chinalipo pa izo; ndi akazi kumathamanga kumeneko, amaliseche mwatheka ndi china chirichonse, ndi kumavina pabwalopo, ndi zinthu; kufika ku mzimu wa kuvinako. Chabwino, uko nkulondola, inu mumalowa mu mzimu wa izo. Ndi mzimu wa mdierekezi. [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndakondwera mwanena kuti, “Ameni,” chifukwa izo nzoona. Ine nditsimikizira izo ndi Baibulo. Uko nkulondola. Chabwino.

<sup>136</sup> Mukuti, “Chabwino, ine sindikukhulupirira izo, m’bale.” Chabwino, inu, si zimene inu mumanena, kapena zimene ine ndikuganiza.

<sup>137</sup> Ndi zimene Mawu a Mulungu amanena. Ndi zimene zimakhazikitsa izo. Amenewo ndiwo Mawu otsirizitsa. Inde, bwana. Iye anati, “Ngati inu mukonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa inu.” Uko nkulondola. Ndipo inu mukukumbukira mkazi wamng’ono uja, wachikulire anamuphunzitsa mwana wake wamkazi kuti azivina, ndi zinthu monga zimenezo, ndipo anapita kumusi uko ndipo anakavina pamaso pa mfumu, ndipo anafuna mutu wa Yohane M’batizi; sevente a ana ake amafa ngati achiwerewere ndi kunyongedwa. Inu mukhoza kuwona chimene chimachita monga chomwecho.

<sup>138</sup> Amayi ake a Mose ankakhala kunyumba, ndipo ankamusunga iye, ndipo ankamuphunzitsa iye Mawu a Ambuye, inu mukuona chimene chinachitika kwa iye ndi ake. Kudzera mwa iye munatuluka . . . Abrahamu, ndi ena otero, ndi kupitirira mmusi.

<sup>139</sup> Chabwino, zimangotengera chimene mukufuna kuchita. Inu, ndinu munthu wochita mwakufuna kwanu. Inu mumachita pa chirichonse chimene mukufuna kuti muchite. Kulondola. Mulungu anayika patsogolo pa munthu, monga munda wa Edeni, Mtengo wa Moyo kapena mtengo wa imfa. Inu mumapanga kusankha kwanu. Mukuona? Chirichonse chimene mzimu wanu umachikonda, ndi chimene inu muti mudye. Zindikirani tsopano. Ndipo iwo anali . . .

<sup>140</sup> Ine ndikufuna kuti ndiwerenge izi kachiwiri tsopano. Iye anali mu Mzimu. Mzimu unabwera pa iye. Iye anayamba kuwona zinthu. Tsopano penyani.

*Ine ndinali mu Mzimu pa tsiku la Ambuye, ndipo ndinamva . . .*

*Ine ndinalowa mu Mzimu pa tsiku la Ambuye, ndipo ine ndinamva kumbuyo kwanga liwu lalikulu, . . . la lipenga, . . .*

141 “Lipenga.” *Lipenga* ndi “kulengeza.” Gabrieli, pa Kudza kwa Ambuye, adzawomba lipenga la Mulungu. Ili linali lipenga la Mulungu likuwomba. Mwa kuyankhula kwina, Iye akukonzekera kulengeza kopita Kwamuyaya kwa dziko lapansi. Lipenga, ilo ndi chiyani? “Kukonzekera. Ine ndikupatsa iwe Vumbulutso la Yesu Khristu, kuti ukalipereke kwa Mpingo. Ine ndidzayankhula ndi iwe, kumene kuti kudzakhale kopita kwa dziko lapansi, kwa iwo amene alandira ndi iwo amene akana.”

142 Lipenga la Mulungu. “Tcheru!” Munthu aliyense, pamene lipenga liwomba, iye amatenga lupanga lake ndi kuyima pa malo, tcheru. Lipenga!

143 Paulo anati, “Ngati lipenga lipereka liwu losatsimikizika, ndani ati adzakonzekere nkondo?”

144 Umo ndi mmene ziriri lero. Oh, m’bale, pamene ine ndiyang’ana pozungulira ndi kuwona mipingo yonse yozizira iyi, yofunda, yosayanjanitsika, ndi zinthu monga zimenezo, “okhala ndi mawonekedwe aumulungu, ndipo nkumakana mphamvu yake,” munthu angadzikonzekeretse yekha motani? Kupereka liwu losatsimikizika.

145 Mukuti, “Chabwino, tsopano, ine ndijowina matchalitchi. Ine ndipita uko ndi kukayesera Methodisti, kapena Baptisti, kapena Chilutera, kapena Chipentekoste. Ine ndikachita chinachake. Ndikapanga mtundu winawake wa kusuntha.” Oh, izo sindizo.

146 “Pokhapokha munthu atabadwa mwatsopano.” Ine sindikusamala kaya iye ndi wa Methodisti, Baptisti, Pentekoste, kapena chirichonse chimene iye ali, inu muyenera mubadwe mwatsopano; inu simudzalowa mu Ufumu. Amen.

147 Taonani,

. . . *liwu*, . . . *la lipenga*,

*Likuti* kwa ine, *Ine ndi Alfa ndi Omega*, . . .

148 Chinthu choyamba kutuluka . . . Iye akupereka malonje apa, “Ine ndine, Woyamba ndi Wotsiriza.” Chinthu choyamba, pamene lipenga la Mulungu linawomba, iye anapotoloka. Ndipo Iye anati, “Ine ndi Alfa ndi Omega. Ndine wochokera ku A mpaka Z. Ndine zonse za zimenezo tsopano. Imani ndipo mumvetsere kwa Ine, kwa kanthawi.” Chabwino.

. . . *woyamba ndi wotsiriza*: . . . *Zimene iwe ukuwona, ulembe mu bukhu*, (limenelo ndi Bukhu ili limene ife tikuliwerenga) *ndipo ulitumize ilo kwa* . . .

149 Kuti? Analemba kwenikweni. Kuti lipite kuti, lipite ku m’badwo? Ayi. “Ku mpingo.” Ku mpingo. Zindikirani.

. . . *Zimene iwe ukuona, zilembe mu bukhu, ndipo ulitumize ilo kwa mipingo isanu ndi iwiri imene ili mu Asiya*; . . .

<sup>150</sup> Chimene, chinali choimira mpingo. Tsopano, ife tilowa mu zimenezo, mu maminiti pang'ono, kuwonetsera momwe Chipangano Chakale chinaimiriridwa mu mibadwo isanu ndi iwiri. Mibadwo isanu ndi iwiri yoikidwa, kapena mipingo isanu ndi iwiri yoikidwa kuno mu Asiya, imene Baibulo momveka limaphunzitsa, imene inali mthunzi, kapena choimira cha Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo imene imabwera. Ndipo mwa thandizo la Mulungu, ndipo ndi Baibulo, tikhoza kutsimikizira kuti m'badwo wa mpingo uliwonse unafika ndendende kumene Ilo linanena kuti iwo udzatero, ndendende basi kumene Baibulo linanena kuti iwo udzatero. Ndipo ife tiri pamapeto a m'badwo wa mpingo wotsiriza.

<sup>151</sup> Ndipo nkubwerera mu Chipangano Chakale, kukatenga loto la Daniele, ndi kumuwonetsa iye masomphenya a ufumu wa Amitundu, momwe iye anawona fano litaima; ndi mutu wagolide, chifuwa cha siliva, ndi ntchafu za mkuwa, ndipo mapazi ndi miyendo yachitsulo ndi dongo. Ndipo anawonetsera momwe uliwonse wa maufumu amenewo umasinthanirana wina ndi umzake, ndendende basi momwe Baibulo linanenera. Ndipo, taonani, mutu wa golide, Babulo; Amedi ndi Aperezi, Agriki; ndi ufumu wa Chiroma; ndipo ufumu wa Chiroma unasweka kukhala maufumu khumi, Roma wakummawa ndi wakumadzulo, ndi zina zotero. Ndipo mmenemo, munali chitsulo ndi dongo, ndipo izo sizimasakanizika pamodzi; Chiprotestanti ndi Chikatolika pansi pa ulamuliro womwe woyewero wa Amitundu. Ndipo iye ananena kuti ngakhale poyesera kuti aphwanye mphamvu ya wina ndi mzake, iwo amakhoza kukwatirana mosakanizikirana wina ndi mzake, ndendende basi zimene iwo akuchita lero, ndendende.

<sup>152</sup> Ndipo ufumu umenewo mmasiku a mafumu amenewo. Mulungu wa Kumwamba anadula Mwala kuchokera m'phiri, popanda manja, umene unadzaphwanya fano ili ku mapazi ndi kuwaswa maufumu onse a Amitundu. Ndipo Ufumu wa Khristu unalamulira ndi kuchita ufumu, ndipo unakula, ndipo unaphimba dziko lapansi ndi nyanja ndi mlengalenga. Maufumu a Amitundu anazimirira ngati dwale, ngati mankhusu pa dwale lopunthira mu nthawi ya chirimwe. Ndi chithunzi chotani chimene ife tikukhalamo. Izo nzoona.

<sup>153</sup> Ndipo lero, inu mmawawona Akatolika ndi Achiprotestanti akukwatirana wina ndi mzake, kuyesetsa kuti aphwasulire mphamvuyo pansi; kulera ana anu, kuchita kulonjeza kuti muwalera iwo mwanjira *iyi* kapena njira *iyoyi*. Ife tifika mu zimenezo, pakapita kanthawi, m'mausiku pang'ono. Tazindikirani zimenezo, momwe izo ziliri, ndi momwe (chinacho) champhamvu chachitsulo chinalamulira pa chimzake, anachiswa icho mzidutswa ndi kuchimwaza icho.

<sup>154</sup> Koma Mwanawankhosa anabwera ndipo anadzaimirira. Ndipo anthu oyera mtsiku limenelo . . .



155 Ndi momwe kuti mphamvu ya Chiroma inafalikira mfuko lirilonse. Palibe mphamvu ina mdziko, ndipo njira imodzi yokhayo imene iyo ingadutsemo, ndi kudzera mu Chikatolika, mpingo wa Katolika, kupita mdziko lonse, kukafalikira mmenemo. Ndi chithunzi chodabwitsa, chachikulu apa.

156 Tsopano, kwa inu Achiprotestanti, ingovalani nsapato zanu, chifukwa, m'bale, inu muli nazo izo. Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira izo mwa Mawu a Mulungu, inu muli kumene mu zimenezo mwa usinkhu wofanana—ndi ena onsewo.

157 Tsopano, penyani tsopano, “Woyamba ndi Wotsiriza. Chimene iwe wawona, chilembe mu Bukhu.” Tsopano, Iye anati kwa iye:

... *lemba ichi mu bukhu, ndipo uchitumize icho ku a... mipingo imene ili mu—mu Asiya; ku Efeso, ndi ku Sarde, ndi... Pergamo, ...ndi kwina kotero, ndi Filadelfiya, ndi... Laodikaya.*

158 Tsopano tiyimira pamenepo, mphindi chabe kapena ziwiri, ndingowona kuti ndiri ndi nthawi yochuluka bwanji, chifukwa ine ndikufuna kuti ndifike ku mfundo yaikulu yotsiriza iyi, pa Efeso, ndi kuyikokera iyo ku Laodikaya, ndi kuwona ngati ife sitiri paubale mu mpingo womwewo, mwaona, tiwone ngati ife sitikukhala mu tsiku lino.

159 Oh, Mpingo wa Mulungu wamoyo, dzukani ndipo muwale. Penyani. Inu simukuzindikira. Ine ndikanakonda ndikanakhala ndi mtundu wina wa kudzidzimutsa umene ine ndikanakupatsani inu, mwanjira yina. Ine ndikanakonda Mzimu Woyera ukanabwera mu mphamvu Yake yayikulu ndi kudzakusunthirani inu pamalo amene inu mungagwire Baibulo ili ndi kunena kuti, “Ndiloreni ine ndiyang’ane mu *Ichi*,” pamene inu mwachiwona:

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,  
Zizindikiro zimene Baibulo linaneneratu;  
Masiku a Amitundu akwanira, ndipo zowawa zachuluka;  
“Bwererani, O omwazikana, kwanu.” (Uko nkulondola.)

Tsiku la chiwombolo layandikira,  
Mitima ya anthu ikulephera chifukwa cha mantha;  
Dzazidwani ndi Mzimu wa Mulungu, nyali zanu zikhale zokonzedwa ndi zowala,  
Yang’anani mmwamba! Chiwombolo chanu chayandikira.

160 Izo nzoona. Oh, ndi tsiku lotani. “Lembani izo, muzitumize izo kwa mipingo.”

<sup>161</sup> Tsopano, chimodzimodzi monga momwe Israeli anadzabwera mu kukongola kwake, mmbuyo pachiyambi pansi pa Abrahamu, anabwera kudzera mwa mbadwa. Ndipo mu tsiku la Ahabu izo zinapita mu mibadwo ya mdima, m'badwo wa mdima kwambiri umene mpingo unawuwona. Anatuluka kunja uko. . . Ndipo mu nthawi imeneyo, momwe Ahabu anakwatirira Yezebeli, anabweretsa kupembedza mafano mu mpingo wa orthodox.

<sup>162</sup> Chinthu chomwe chomwecho, kuti, Chiprotestanti chinakwatira Chiroma mu zaka fiftini handiredi za mibadwo ya mdima, mu Mpingo wa Pergamo, ndipo unatulukamo ndi kupembedza mafano, pansi pa mawonekedwe a Chikhristu, kupita mu m'badwo wofunda umene ukubwera patsogolo pathu. Ndipo ife tiri mmenemo pakali pano. Ife tiri mu m'badwo wofunda.

<sup>163</sup> Inu simukukhulupirira zimenezo? Tsopano ine ndikhala pansi pa. . . anthu inu kunja mmatchalitchi ena. Inu muli mu m'badwo wofunda. Ndipo avangeli anu akudutsa mdziko lapansi, kuzungulira dziko lapansi, akulalikira zinthu ngati zimenezo; inu simukupita nazo patali. Inu mukumakuwa. . . Inu Abaptisti mukumakuwa, "Millioni enanso mu '44." Inu mupeza chiyani mukawapeza iwowo? Mungokhala ndi gulu la ochimwa amene abwera, ali ndi maina awo pa bukhu (Uko nkulondola.), kumati iwo ndi a mpingo wa Baptisti. Osati iwo okha, koma enanso, Amethodisti, a Campbellite, ndi gulu lonselo, ofunda basi ndi osayanjanitsika. Billy Graham anali nazo zimenezo, "Otembenuka sarte sauzande," iye anati, "mu masabata sikisi. . ." Ndipo masabata sikisi kenako iye sanakhoze kuwapeza sarte. Bwanji? Bwanji? Iwo sanapeze kalikonse, kuyamba ndi kuyamba. Basi gulu la ochimwa, chikhalirenicho anayika dzina lawo m'bukhu, pansi pa kutengeka kwa chitsitsimutso.

<sup>164</sup> Iye anati, "Ufumu wa Kumwamba uli ngati iye amene anaponya ukonde, mnyanja. Pamene iye anawukocheza, iye anakola chirichonse." Iye anali atakola akamba. Iye anali atakola nkhanu. Iye anali atakola nkhasi. Iye anali atakola kangaude. Anali atakola tizilombo ta mmadzi. Iye anali atakola njoka. Uko nkulondola. Koma mmenemo, iye anali atakola nsomba zina, aponso.

<sup>165</sup> Ndipo pamene munthu alalikira chitsitsimutso pansi pa mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera, ukonde umakokedwa pa anthu. Uko nkulondola. Koma ngati iye ali kachilombo kuyamba ndi kuyamba, iye amakhala kachilombo pa kutha kwa chitsitsimutsocho.

<sup>166</sup> Ngati iye ali kangaude wa mmadzi, chinthu choyambirira inu mukudziwa, iye azipita kumakafufuza pozungulira, kumati,

“Ine sindikhulupirira mu zinthu zakale izi mulimonse,” ndi kumabwereranso mmadziwo.

<sup>167</sup> Ngati iye ali njoka, iye adzati, “Ine ndinakuuzani inu za izo,” ndipo kutali iye adzapita. Iye anali njoka kuyamba ndi kuyamba, chikhalidwe chake chinali. Ndipo iye sadzakhala china chirichonse kufikira chikhalidwe chimenecho chitasinthidwa.

<sup>168</sup> Munthu sangakhoze kujowina tchalitchi, kapena kukhala wotengeka, kapena china chirichonse, nkudzakhala Mkristu. Izo ziyenera kukhala kubadwa kokhazikika kwa Mzimu; kuwonamtima, kufa, kumalira mofuula, kugona pamenepo mpaka iye atafa kawiri. Kumbukirani, moyo umangokhoza kutulukira chinthu chikafa.

<sup>169</sup> Njere ya chimanga, ngati ingokhala, iyo imakhala yokha, iyo siidzatanthauza chinanso kuposa njere imodzi iyo ya chimanga. “Pokhapokha njere ya tirigu itagwera mu nthaka, iyo imakhala yokha.” Koma pamene iyo igwera pamenepo, iyo imawola, imavunda, ndipo kuchokera mkati mwa chivundi chimenecho pamabwera nyongolosi ya moyo imene imaipatsa iyo moyo ndi kubereka zochuluka.

<sup>170</sup> Pokhapokha mpingo utabadwa mwatsopano, kufa ku tizikhulupiriro take ndi zaumulungu, ndi zina zotero, ndi kubadwa mwatsopano ndi Mzimu wa Mulungu, iwo udzakhala wakale, wozizira, wofunda, wopanda umulungu, wosayanjanitsika. Amen. Uko nkulondola. Kumeneko ndi kulalikirira kwachikale, kwachimidzi, koma iko kudzakupulumutsani inu, m’bale. Uko nkulondola. Iko kudzakusungani inu pamene mikuntho ikuwomba mwamphamvu. Kuzikika ndi kukhazikika. Mupale nyansi zonse musanathire konkireti yanu; zindikirani, uko nkulondola, ndipo nangula amatsika bwino bwino ndipo molimba. Oh, m’bale, ndi tsiku lotani limene ife tikukhalamo; m’badwo wa mpingo wofunda, wosayanjanitsika! Inde, bwana.

“Kwa mipingo isanu ndi iwiri,” anati, “tumizani uthenga uwu.”

<sup>171</sup> Tsopano, mu m’badwo wa mpingo umenewo, iwo anayamba kumabwera; iwo anakwatira mu kupembedza mafano. Iwo akuchita chinthu chomwe chomwecho tsopano; iwo abweramo, akuchita chinthu chomwe chomwecho. Ndipo kuchokera mmeneno, pakubwera Chikristu chofunda, chinayamba kuzimirira mpaka ife tikufika ku m’badwo wa mpingo wotsiriza.

<sup>172</sup> Tsopano, mpingo wamakono, umene ife timawutcha “chipembedzo.” Ife anthu a chiyero, inu mukudziwa, timawutcha iwo, “amakono,” ndipo iwo amapita kunja uko ndipo iwo amakayamba chitsitsimutso chawo, nawonso. Inu mukuti, “Iwo sakupita kulikonse.”

<sup>173</sup> Koma tsopano dikirani miniti yokha. Kodi ife tiri ndi chiyani? Tiribe kalikonse, osati mochuluka kuposa momwe

iwo aliri. Ndiko kulondola ndendende. Bola ngati ife tikumakangana ndi kudyana ndi kumapitirira pa wina ndi mzake, ife tikumayendabe ngati amuna; kufikira munthu atafika pa guwa ndi kukakonzana ndi Mulungu, kufikira iye atamazilambalala zinthu zazing'ono ndi kumasuntha chitsogolo monga Mkhristu ayenera kuchitira. M'phika sungakhoze kutcha ketulo noninoni. Kulondola. Musamawafuulire iwo. Tiyeni tiziyeretsa mayendedwe athu omwe poyamba.

<sup>174</sup> Mutikhulukukire ife, alendo, ine ndikuwupatsa mpingo kukwapula pang'ono kwa Uthenga tsopano. Zindikirani, uko nkulondola. Ndizo ndendende zimene inu mukusowa.

<sup>175</sup> "Oh," inu mukuti, "ife tiri nawo Iwo." Ndipo nkufika pamwamba apo ndi kumayimba limba mwamphamvu momwe iyo ingalirire, ndi mulu wa ng'oma, ndi kumathamanga thamanga pamenepo, ndipo kutuluka ndi kumakakangana ndi woyandikana naye wanu. Kodi inu muli ndi chirichonse? Uh-huh. Ayi, bwana. Chinthu chokhacho chimene ife tiri nacho ndi kufunda. Bola ngati nyimboyo ikulira, ife tikuthamanga. Nyimbo ikayima, ife timayima. M'bale, musamamutchule munthu winayo chinachake; tiyeni tiyang'ane pozungulira khomo lanu lomwe, choyamba. Amen.

<sup>176</sup> Ine ndikukuuzani inu, ife tikusowa chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale monga ife tinkakhalira nacho uko kumudzi, pamene iwo ankagona chafufumimba usiku wonse. Osati kumapitirira, koma pamene chisoni chenicheni chaumulungu; ndipo osabwerera ku guwa ndi kukakhala, koma kutuluka ndi kukakonzana ndi oyandikana nawo amene iwo analakwirana nawo, ndi kufika pokonzedwa. Inu mukudziwa kuti uko nkulondola. Zikuwotcha, koma, m'bale, izo zikuthandizani inu. Uko nkulondola. Inu mukuyenera kudziwa zimenezo, mzanga. Inde, bwana.

<sup>177</sup> Kufunda, chimenecho ndi chikhalidwe choyipa kuti mpingo ukhalemo. Inu simukusamalitsa, Branham Tabernacle ili pafupifupi mu kupepeluka komweko. Mvetserani, inu mukuzidziwa zinthu zimenezi. Izo zakhala zikuphunzitsidwa, chaka ndi chaka, ndi chaka, ndi chaka, pa nsanja ino, kukuchenjezani inu za zinthu izi kuti zikubwera. Pamene, Baibulo linati idzakhalapo nthawi imene iwo ati azidzapita kuchokera kummawa kupita kumadzulo, ndi kumpoto ndi kummwera, kuyesetsa kuti apeze Mawu owona a Mulungu, ndi kulephera kuti awapeze Iwo. Inu kulibwino mukhale ozikika, pamene inu mukudziwa pamene inu mwayima.

<sup>178</sup> Koma pamene munthu abadwa mwatsopano kamodzi; osati kungotentheka, osati kutengeka kwina, osati pa kuika dzina lake mu bukhu la mpingo, osati pa kujowina mpingo wawukulu kwambiri mu mzinda. Koma pamene iye walira kwenikweni, ndipo wapempha, ndi misozi mmaso mwake, kufikira Mulungu

atakhulukira machimo ake, kuyeretsa solo yake ku moyo wa tchimo, ndi kumudzaza iye ndi Mzimu Woyera; ndi chikondi choterocho, ndi mwaumulungu, kufikira iye atatengera zida zakale za matayala izo nkukazibweza, zimene iye anaba kwa oyandikana nawo, ndipo nkupita ndi kukakonzza zinthu izi, ndi kumakakhala waumulungu pamaso pa anthu. Ife sitidzakhala konse ndi chitsitsimutso mdziko lino mpaka ife titakhala ndi zimenezo.

<sup>179</sup> Chiweruzo chimayambira mnyumba ya Mulungu, ndi Mawu a Mulungu. Amen. Osati bukhu lophunzirira, koma Baibulo. Osati zimene mpingo wina umaphunzitsa mu zaumulungu zawo, koma zimene Mulungu amanena. Zikatero inu mudzakhala ndi chitsitsimutso kumene mphamvu zazikulu, ndi zodabwitsa, ndi zizindikiro, ndi zozizwitsa, ndi china chirichonse, zizidzachitika.

<sup>180</sup> Ndife ofunda. Chifukwa ndife ofunda mu m’badwo uno, Mulungu anati, “Ine ndidzakulavulani inu kuchokera mkamwa Mwanga.” M’badwo wa mpingo uno udzakanidwa. Padzakhala otsalira a iwo, amene ati adzapulumutsidwe. Chotero kulibwino muzilembe nokha, mwabwino ndithu, kuti mudziwe ngati inu muli mwa otsalirawo tsopano. Ife tilowa mu zimenezo mu miniti, ngati Mulungu alola. Mungozindikira tsopano.

*Ndipo ine ndinatembenuka kuti ndiwone liwu limene linayankhula ndi ine. Ndipo pamene ndinatembenuka, (Penyani.) Ine ndinawona zoyikapo kandulo seveni zagolide; . . .*

<sup>181</sup> Kapena, “zoyikaponyali,” Agriki amatero. Tsopano, ndiko kumasulira koyambirira, chifukwa iwo sankakhala ndi makandulo ndi. . . Iwo ankakhala ndi choyikapo nyali chaching’ono. Tsopano, Zoyikapo Nyali Seveni Zagolide, ife timadzitcha izo.

<sup>182</sup> Tsopano, mmalo oyerera, kumene mkate wopanda chotupitsa; ndipo ambiri a inu azibusa mukumvetsa, ndi zimenezo. Ndipo anthu inu pano pa kachisi, pokhala kuti mukuphunzitsidwa ndi mphunzitsi wabwino kuno, inu—inukuzidziwa zinthu izi.

<sup>183</sup> Zoyikapo Nyali Seveni Zagolide, izo zinali. . . zinali ndi nyali zazing’ono pamwamba pa izo, zimene zinkayatsa mafuta. Uko mu Zakariya, kumene iye anawona masomphenya, ine ndikukhulupirira ndi kumeneko, ndipo iye anawona mtengo wa azitona wakuthengo ndi mtengo wa azitona wapakhomo; Myuda ndi Wamitundu, kale isanafike nyengo ya Amitundu. Iwo ankakhala ndi zofukizira zagolide, ndipo zofukizira zagolide zonsezi zinkalowa mu choyikapo nyali chimodzi ichi apa chimene chinkapereka mafuta kwa nyali zonsezo. Ndipo iye samamvetsa momwe zinthu izi zimakhallira; mtengo wakuthengo wa azitona ndi mtengo wa azitona wapakhomo. Ndipo mtengo

wa azitona wapakhomo, ndithudi, unadulidwa, ndipo mtengo wa azitona wakuthengo unamezanitsidwa mwa iwo.

<sup>184</sup> Ndipo mafuta amenewo a nyali, *mafuta* amaimira “Mzimu Woyera,” nthawizonse. Ife tifika mu zimenezo, pa kuwalemba chisindikizo anthu, Lachisanu usiku. Zindikirani, koma mafuta awa akuyimira Mzimu Woyera. Ndi chifukwa chake ife timawadzoza odwala ndi mafuta, ndi chifukwa chakuti iwo amaimira Mzimu Woyera.

<sup>185</sup> Baibulo linatero, mu Chivumbulutso mutu wa 6, pamene mliri unapita, iye anati, “Muyeso wa tirigu mtengo wake rupiya, ndi miyeso iwiri ya balere mtengo wake rupiya; koma usawononge vinyo Wanga ndi mafuta Anga.” Ndikanakonda ife tikanati titenge Chivumbulutso mopitirira, kwa masabata angapo, ndi kulowa mu zimenezo, chimene vinyo ndi mafuta ameneyo ali. “Uwone kuti usaipsye vinyo Wanga ndi mafuta Anga. Usayandikire izo.” Amen.

<sup>186</sup> Tsopano, zindikirani zoyikapo nyali zagolide izi. Mafuta awa ankatsanuliridwa mu zoyikapo nyali izi. Tsopano, mafuta anali amene ankaikidwa mu nyali, kuti ziziyaka. Tsopano, Aroni anali . . . Inali ntchito yake kuti aziyatsa nyali zimenezi. Ndipo nyali izi zinkayenera kuyatsidwa. Gwiranibe izi tsopano. Penyani. Khalanibe a ulemu, ndipo mvetserani. Nyali izi zinkayenera kuyatsidwa ndi moto umene Mulungu anauyatsa. Ana a Aroni amalowamo ndi moto wachirendo, ndipo Mulungu anawaphera iwo pakhomo; uko nkulondola, moto wachirendo. Moto umene Mulungu anawuyatsa!

<sup>187</sup> Ndipo penyani, tsopano, zoyikapo nyali zimayenda mwa uta. *Apa* panali choyikapo nyali chimodzi, ziwiri, zitatatu, zinai (kumakwera), zisanu, zisanu ndi chimodzi, zisanu ndi ziwiri, monga *chonchi*. Tsopano, zoyikapo nyali zagolide izo apa, monga iye akunenera mmaminiti ochepa.

<sup>188</sup> Tiyeni tiwerenge mopitirira pang’ono, mwinamwake timvetsa izo. Ndipo mvetserani chimene iye ananena tsopano. Chabwino. “Ndipo mutu Wake . . .” Ine ndikukhulupirira kuti ndapita patsogolo pa ndime ya 12 pamenepo, “Zoyikapo Nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide.” Ndime ya 13:

*Ndipo pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide wina wonga. . . Mwana wa munthu, atavala chovala chofika kumapazi, ndipo atamanga lamba wagolide pachifuwa.*

*Mutu wake unali ngati—ngati. . . tsitsi lake linali loyera ngati ubweya. . . woyera ngati chipale; ndipo maso ake anali. . . malawi a moto; . . .*

<sup>189</sup> Tsopano, tiyeni tiyimire pamenepo miniti yokha, chifukwa ife sitingachisiye chithunzi chimenecho pamenepo monga chomwecho. Tayang’anani pa zoyikapo nyali izi zayima apa tsopano. Chabwino, zoyikapo nyali izo, monga momwe ife titi

tizipezere mtsogolo pang’ono, zikuimira Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo. Izo zikuimira Aefeso, Pergamo, ndi kumatsika mmusi mpaka ku Filadelfia, ndi kupitirira mpaka ku Laodikaya; Mibadwo Isanu Ndi Iwiri Ya Mpingo.

<sup>190</sup> Ndipo chirichonse cha zoyikapo nyali zazing’ono izi chimakhala ndi supa ya mafuta itakhala pamenepo, ndipo mafuta awa ankayaka pa nyali iyi. Tsopano pamene nyali imodzi iyatsidwa ndi moto wa Mulungu, iwo amaitenga nyali imeneyo ndipo amakaiyatsa inayo, kenako nkuyisiya iyo pansi; ndi kuyatsa inayo; ndipo imodzi imayatsa inayo, kupita pa imzake, kupita pa imzake, mpaka nyali yotsiriza. Zindikirani, mafuta omwewo.

<sup>191</sup> Tsopano, Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo iyi, inayamba ndi Aefeso, ndi Tiyatira, Pergamo, ndi kumapitirira. Ndipo Mzimu Woyera, umene uli Mafuta a Mulungu, unagwera pa mpingo pachiyambi, mu Aefeso, Mpingo wa Aefeso, umene unali mpingo wa chisomo. Inu Abaptisti mukuyenera kufuula “ameni” pamenepo. Ndipo kenako pa mpingo wa chisomo, umene mu Efeso, ndipo kalata ya Aefeso imatiika ife poyera, omwe ife tinali maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Iwo unagwa kumeneko, ndipo iwo analandira Mzimu Woyera.

<sup>192</sup> Koma dikirani miniti, m’bale wanga wa Baptisti, kodi iwo anawulandira motani Iwo? Kodi iwo anawulandira motani Iwo? Mwa kujowina mpingo? Zosatheka. Iwo anawulandira Iwo mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Inu mukuti, “Inde, M’bale Branham, uko nkulondola.” Chinachitika ndi chiyani kwa inu pamene Iwo unagwera pa inu?

<sup>193</sup> Zindikirani, Moto womwewo umene unawotcha mafuta uko, mu Efeso, unawotcha iwo mu Tiyatira; Moto womwewo unawotcha kumeneko, unawotcha iwo mu Pergamo; unawotcha kumatsikira pansi ukudutsa, mpaka ku M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Mzimu Woyera womwewo, woyatsidwa ndi Mulungu yemwe yemwewo, ndi Moto womwe womwewo. Ndipo Moto umene unadzagwa pa Pentekoste unayatsa kandulo, Mpingo, kudutsa mu m’badwo uliwonse, mpaka pansi tsopano.

<sup>194</sup> Koma vuto lake ndi lakuti, ife Abaptisti, ife Amethodisti, ife tiri mmbuyo momwe *kuno*, tikuyesetsa kuti titenge chinthu china cha mbiriyakale, ndipo apa Mpingo ukupita kumusi *kuno*. Uko nkulondola. Apo ndi pamene ife tatsalira. Mpingo uliwonse, pamene iwo un kayamba, kunalibe. . .

<sup>195</sup> Tayang’anani pa Lutera, mu kukonzanso koyamba. Ndi chitsitsimutso bwanji, Lutera. Taonani, ine ndiri nalo bukhu lake kunyumba. Momwe munthu ameneyo anagwedezera pansi pa mphamvu ya Mulungu! Momwe iye ankakhulupirira mu machiritso Auzimu, anawalandira Iwo mwiniwake; ankakhulupirira mu mphamvu ya Mulungu, ngakhale mochulukwa kwambiri, mpaka iye anayankhula mu malirime,

Marteni Lutera. Ndiko kulondola ndendende. Marteni Lutera ankayankhula mmalirime.

<sup>196</sup> Ndipo kenako m’badwo wotsatira unadzabwera, John Wesley. John Wesley anadzachita chinthu chomwecho. Pamene iye ankalalikira, iye anati, “Mawu awa ndi otani amene ine ndikuyankhula, osadziwika kwa inemwini?” Uko nkulondola, amayankhula ndi malirime; ankakhulupirira mu machiritso Auzimu. Ndipo pamene iye anabwera ku Amerika, mipingo kuno inamuchitira iye monga iwo amachitira ndi oyera odzigudubuza lero, iwo ankamutulutsa iye, mmatchalitchi. Ndipo iwo ankalalikira Uthenga kunjira uko, ndipo anagwa pansa pa mphamvu ya Mulungu, mpaka iwo ankagona pansa, usiku wonse pa nthawi.

<sup>197</sup> Ndipo bukhu kumene la John Wesley, limene ine ndiri nalo kunyumba tsopano, la limene iye ankakwera kavalo tsiku lina, kuti akapempherere mkazi yemwe ankadwala, ndipo kavaloyo anagwa ndipo anathyola mwendo wake. Ndipo iye anatsika pa kavalo, ndipo anatenga nsupa ya mafuta ndipo anamudzoza kavaloyo ndi mafuta, ndipo anakwera pa iye ndipo ananyamuka. Moto womwewo ukuyaka pamene.

<sup>198</sup> Koma inu mwazifikitsa izo ku mawonekedwe a mwambo wa chinachake, ndipo Mzimu Woyera ukusunthabe. Kulondola. Uko nkulondola.

<sup>199</sup> Ndipo mu mpingo wa Methodisti, “Iwo ali ndi chinachake cholakwika ndi izo,” mwa- . . . bukhu lawo linati, “iwo amakhala ndi kuzigwedeza.” Ndipo akayamba kuti aziyenda, ndipo iwo amakhoza kuzigwedeza ndi kulumpha, ndi kumachita monga *chomwecho*, mmisonkhano yawo ya mmahema ndi zinthu, Amethodisti. Bwanji, m’bale, ngati John Wesley angakhoze kuwuka powonekera, iye akhoza kuchita manyazi kwambiri ndi inu, iye angakukaneni inu; pokhapokha atakukwapulani inu ndi chikwapu chabwino cha Uthenga ndi Uthenga umene iye anawulalikira.

<sup>200</sup> Ine ndinaima osati kale kwambiri, pafupi ndi kachisi, kumene iwo anawamasula agalu amenewo, tsiku limenelo pamene iye ankalalikira a—kubadwa kwatsopano, ndi zina zotero, ndi zimenezo. Ndipo mpingo wapamwamba wa England unawamasulira agalu amenewo pa iye. Ndipo iye anati, “Dzuwa siligwa pa mutu wanu katatu, mpaka inu mutandiitana ine kuti ndimupempherere iye.” Ndipo iye anatero; ndipo anafa. Uko nkulondola. Ndithudi.

<sup>201</sup> Icho ndi chimene ife tikuchisowa lero. Ife tikusowa mtundu umenewo wa Chimethodisti. Tikufuna wa Baptisti wina ngati John Smith, amene ankakhala mchhipinda ndi kumamudandaulira Mulungu, ndipo anapemphera usiku wonse, mwanjira imeneyo, kufikira kuti maso ake anatupa moyipa



kwambiri, mmawa, mkazi wake ankachita kumutsogolera iye popita ku tebulo, kuti akadye.

<sup>202</sup> Oh, kodi ife tikuchita chiyani lero? Timayima pangodya, tiri ndi ndudu pakamwa pathu; ndipo mdikoni mu tchalitchi, ndipo nkupita uko ndi kumakachita; ku makanema, ndi kumakawonera ma televizioni usiku wonse; ndipo nkumajomba osapita ku tchalitchi; kumasuta, kumwa, kumatchova njuga, kumakathamanga ku mijaha ya akavalo, ndi kumadzitcha tokha Abaptisti. Zonsezo nyansi!

<sup>203</sup> Chimene ife tikuchisowa lero ndi chitsitsimutso china chachikale, chotumizidwa ndi Mulungu, cha Mzimu Woyera. Ameni. Ine sindikutanthauza... Ine sindikuyesera kuti ndikupangitseni inu kuti musangalale. Ine ndikudziwa kuti simukusangalala, koma, m'bale, icho ndi choonadi. Ndikuyesetsa kuti ndifikitse mfundoyo kwa inu. Ndicho choonadi. Ndi chimene ife tikuchisowa. Chabwino.

<sup>204</sup> Tsopano, limenelo ndi Baibulo. Ndicho chimene Mzimu ukunena, mwaona. "Zoyikapo nyali." Chabwino. Tsopano ndime ya 13.

*Ndipo pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide wina wonga... Mwana wa munthu,...*

<sup>205</sup> Chiyani? Mmodzi wonga Iye. Kodi ameneyu anali ndani? Mkwatibwi Wake. Mmodzi wonga Iye. Penyani momwe izo zinakhaira.

*... atavala chovala chofika kumapazi,...*

<sup>206</sup> Chiyero cha Yesu Khristu chikumuphimba Iye. "Watitsuka ife ku machimo athu ndi Magazi Ake Omwe." Chabwino.

*... atamanga lamba pachifuwa (osati mwamuna; mkazi) ndi lamba wagolide. (Uthenga umene unali ndi mphamvu ndi ulemelero wa Mulungu pa Thupi la Khristu.)*

<sup>207</sup> Oh, ndi chithunzi chokongola bwanji chimene ife tiri nacho apa kuti tichilingalire. Tayang'anani apa.

*... mpaka kumapazi, ndipo atamanga lamba wagolide pachifuwa.*

*Mutu wake ndi tsitsi lake zinali zoyera ngati ubweya, ... zoyera ngati chipale (chirungamo, chiyero; kuyera kumayankhula za izo); ndi maso ake... ngati malawi a moto; (Amayang'ana kudzera mwa iwo.)*

<sup>208</sup> Musayesere kuti mumubisalire Iye. Iye amadziwa yemwe inu muli, kumene inu muli, ndi chimene inu mwachita. Inde, bwana. Iye amawona chirichonse. O Mulungu...

<sup>209</sup> Ife tangotsala ndi maminiti pang'ono chabe ngati ine ndingafike ku m'badwo wa mpingo wina uwu, ngati ife tingathe. Zindikirani.

*Ndipo mapazi ake anali ngati . . . mkuwa wabwino, . . .*

<sup>210</sup> *Mkuwa* nthawizonse ndi “chiweruzo,” inu mukudziwa; guwa la mkuwa, ndi njoka yamkuwa, ndi zina zotero. Mkuwa umayankhula za chiweruzo. Mapazi Ake, ndiye, Mpingo wa Yesu Khristu unakhazikitsidwa pa chiweruzo Chauzimu. Khristu kufa mmalo mwathu, Mmodzi Wolungamayo kulipira chiweruzo chathu kumeneko, ku . . . pamaso pa Mulungu, ndipo anafera pamenepo ngati wochimwa pa mtanda, ndipo moyo Wake unakwera kupita ku gehena. Ndipo Mulungu, osalola kuti Mmodzi Wake woyera awone chivundi, anamuukitsa Iye pa tsiku lachitatu, kwa kulungamitsidwa kwathu; Yemwe akukhala pa dzanja Lake lamanja tsopano, Wansembe Wamkulu akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu; amene adzabwerera momwemo monga Iye anapitira Kumwamba, kuti akalandire Mpingo waulemelo umene wadzikonzeke Wokha, wotsukidwa ndi Magazi ndi wobadwa kachiwiri. Ndi a—masomphenya bwanji. Amen. Chabwino. “Monga mkuwa wabwino,” kapena, penyani tsopano, “ndi Ake . . . ndi . . .”

*Ndipo mapazi ake anali ngati . . . mkuwa wabwino, ngati kuti iwo unali utatenthedwa mu ng'anjo; (Ndiko kuti litsiro lonse kuchotsedwapo.) ndi liwu lake . . . liwu la madzi ambiri.*

<sup>211</sup> Penyani, ndi Mpingo ukuyankhula kwa Iye tsopano, *madzi*. Chivumbulutso 17:15, anati, “Madzi amatanthauza khwimbi ndi unyinjwa wa anthu.” Tsopano, “Liwu lake,” kapena Munthu uyu amene anayima pamenepo akuwoneka monga chonchi, Khristu mu Mpingo Wake, monga Mkwatibwi ndi Khristu kukhala Mmodzi, monga mwamuna ndi mkazi ali mmodzi; Mpingo ndi Khristu akuwumbidwa pamodzi ndi Munthu mmodzi, Mzimu Woyera womwewo.

<sup>212</sup> Ndipo zinthu zimene Khristu ankachita, Mpingo ukuzichitanso. Kodi inu mukuziwona zimenezo? Mpingo wokongola uja pamenepo mu chiyero, mu mphamvu, mu ulemelo, ndi kumawona masomphenya, zizindikiro, zodabwitsa. Chirichonse chimodzimidzi monga Iye ankachitira, apa iwo uli pa dziko lapansi; ukupereka matamando onse kwa Mulungu, ukuti, “Sindingathe kuchita kanthu pokhapokha Atate atandiwonetsa Ine; koma Iye wandiwonetsa Ine, ndipo ndi izi apa.” Ndipo ife tikubwera, mwaona, zinthu izi zikuyamba kuchitika.

<sup>213</sup> Tsopano, Khristu, anawumbidwa kukhala Mmodzi.

*. . . ndipo liwu . . . la madzi ambiri . . .*

Anthu ambiri, osati mmodzi yekha; unali Mpingo wonse, Mpingo Isanu Ndi Iwiri itawumbidwa pamodzi mu Thupi limodzi lalikuli lowomboledwa la Ambuye. Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, onse amene abadwa mwatsopano ndi

Mzimu Woyera, akuyankhula ndi mphamvu ya Mulungu, ndiro Thupi. Ndiro Thupi.

*Ndipo iye anali nazo lakumanja kwake. . .*

<sup>214</sup> “Kumanja.” Chirichonse mu Baibulo chimakhala ndi tanthauzo kwa icho, mwaona.

*. . . mu dzanja lake lamanja nyenyezi zisanu ndi ziwiri (tsopano Iye—Iye ndi Mfumu): ndipo kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga lakuthwa konsekonse: ndipo nkhope yake inali ngati dzuwa lowala mu mphamvu yake.*

<sup>215</sup> Tsopano, “Mkamwa Mwake mukutuluka lupanga lakuthwa konsekonse,” kuchokera mkamwa mwa Uyu anayima pamenepo, Khristu ndi Mpingo ngati mmodzi.

<sup>216</sup> “Mdzanja Lake Iye ananyamula nyenyezi zisanu ndi ziwiri.” Ndipo inu muwona mu maminiti pang’ono; ine ndikufuna kuti ndifike ku zimenezo, ndilisiye Baibulo lingoyankhula chimene izo zinali. Iwo anali atumiki asanu ndi awiri, mtumiki mmodzi kwa m’badwo uliwonse wa Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo iyi, akutulukira, anawanyamula iwo mdzanja Lake lamanja. Amen. Ndi Uyo pamenepo. Panali angelo asanu ndi awiri, amthenga asanu ndi awiri, mmodzi ku mpingo uliwonse. Mukumvetsa zimenezo?

<sup>217</sup> Apo, Iye wayima pamenepo.

*. . . ndipo kuchokera mkamwa mwake munatuluka lupanga lakuthwa konsekonse: . . .*

Kodi lupanga lakuthwa konsekonse ndi chiyani? Ahebri mutu wa 4, anati, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ngakhale kupita mmafuta a mmafupa, ndi Wozindikira maganizo a mmalingaliro.” Chabwino.

*Ndipo pamene ndinamuwona iye, ndinagwa pa anga. . . Ndinagwa pamapazi ake ngati wakufa. Ndipo iye anayika dzanja lake lamanja pa ine, akuti. . . Usawope ayi; Ine ndine woyamba ndi wotsiriza:*

*Ine ndine iye amene ndiri moyo, ndipo ndinali wakufa; ndipo, taonani, ndiri wamoyo kwa nthawizonse, Amen; ndipo ine ndiri ndi mafungulo a gehena ndi. . . imfa. (Ameneyo ndi Yesu. Tsopano penyani.)*

*Lemba zinthu izi zimene iwe wazona, ndi zinthu zimene ziripo, ndi zinthu izi zimene zidzakhale mtsogolo; (Chabwino.)*

*Ndipo chinsinsi cha nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene unaziwona mdzanja langa lamanja, ndi. . . dzanja, ndi zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide. Nyenyezi*

*zisano ndi ziwirizo ndi angelo asanu ndi awiri a mipingo isanu ndi iwiri. . .*

218 Ooh! Gwirani zimenezo. “Angelo asanu ndi awiri ndi atumiki asanu ndi awiri a mipingo isanu ndi iwiri.” Kunali mpingo wa mtsogoleri wa ku Efeso. Tsopano ngati Mulungu angalole, ndipo ife nkudzapitiriza ndi izi, ndipo osatenga *Chilemba Cha Chirombo*, ine ndidzakhocha kukuwonetsani inu aliyense wa iwo, mpaka ku m’badwo wotsiriza uno, njira imene—njira imene iwo anali; kukuwonetsani inu Mpingo wa Filadelfia, umene unali wa Amethodisti, John Wesley; kukuwonetsani inu—Mpingo wa Tiyatira, mwamsanga ukangotha wa Pergamo; yemwe anali Martin Luther, ndipo nkupitabe mpaka mmusi mu m’badwo, ndi kuwonetsera aliyense wa iwo amene anabwera ndi kubweretsa uthenga, anadzakhazikitsa uthenga pa dziko lapansi.

219 Ndipo mpaka ku Uthenga wotsiriza, lero, ndiko kulondola, kumene Mulungu anatomiza Mngelo wochokera Kumwamba, anamutsimikizira wantchito Wake, ndipo anatomiza Uthenga kwa aliyense. Uwu sudzakhala mpingo. Iwo sudzakhala bungwe mmasiku otsiriza ano. Chifukwa, Mulungu waliyika bungwe pa alumali, ndipo nonse a inu mukuzidziwa zimenezo. Ndipo dikirani kufikira ife titadzamaliza mawa usiku, pa *Chilemba Cha Chirombo*, ndipo nkudzawona pamene mpingo wanu uli, mwaona, ndi bungwe lanu.

Tsopano penyani mipingo.

*. . .ndipo zoyikapo nyali zisano ndi ziwiri zimene iwe wazionazo ndi mipingo isanu ndi iwiri. (Iyo ndi mipingo.)*

220 Ndipo *nyenyezi*, zimene, Iye wanyamula nyenyezi iliyonse. Tsopano tapenyani. Kodi ife tingangoyima miniti? Ine ndikudziwa kuti ndatsala ndi maminiti thwelofu kuti ndipite apa ndipo ine ndikufuna kuti ndifike pa mutu uwu pomwe pano, ndi kuwerenga iwo, ngati palibe china. Ine ndikufuna ndipereke izi kwa inu. Nyenyezi inali mtumiki, ndipo mtumiki wodzowedwa ndi Mzimu wochokera Kumwamba.

221 Kodi inu mukuzindikira kuti inu mumamirira nyenyezi Kumwamba, ndipo nyenyezi iliyonse Kumwamba imakuimirani inu? Kodi inu mukudziwa kuti Mulungu anamuuzza Abrahamu kuti mbewu yake idzakhala ngati nyenyezi za Kumwamba? Poyamba iwo anali fumbi la dziko lapansi, ndipo kenako mu chiukitsiro iwo anali nyenyezi za Kumwamba, zosawerengeka. Kodi inu munazindikira zimenezo?

222 Kodi inu mumadziwa kuti Yesu anali Nyenyezi Yowala ndi ya Mmawa, Nyenyezi yopambana ya nyenyezi zonse za Kumwamba? Oh, Aleluya! Ndikaganiza za zimenezo, mzimu wanga umalumpha ndi chisangalalo. Ndi Uyo apo! Apo mmawonekedwe Ake, mu Kukhalapo Kwake, ife tidzakhala

tsiku lina, Aleluya, pamene zinthu za dziko lapansi lino zidzapita.

223 Koma, mvetserani, Lemba lina likubwera kwa ine. Daniele anati. . . Pamene Iye anati, “Tsekera. . .”

224 Pamene iye anamuwona Mngelo uyu atatsika pansu, ali ndi utawaleza pa mutu Wake; atayika phazi limodzi pamtunda, ndipo lina panyanja; ndipo anakweza mmwamba manja Ake, ndipo analumbira pa Iye amene ali moyo ku nthawi za nthawi. Pamene maliwu asanu ndi awiri amenewo anayankhula awo. . . Mabingu Asanu Ndi Awiri anayankhula maliwu awo. Iye anati, “Sindikiza izo; osadziwika kufikira tsiku lotsiriza.” Iye anati, “Koma nthawi imene chinsinsi cha Mulungu ichi chiti chidzamalizidwe, pamene izi zizidzawululidwa kwa Mpingo; ndipo analumbira pa Iye amene ali moyo kwanthawi za nthawi, kuti nthawi kulibenso.”

225 Mvetserani chimene Iye ananena pamenepo ndiye. Iye anati, “Pita panjira yako, Daniele, tsekera Bukhulo.” Mukuona? “Pakuti iwe udzapumula, ndipo udzayima mmasiku otsiriza, pa malo ako. Koma ambiri a iwo amene adzatembenzira ambiri ku chilungamo adzawala kuposa nyenyezi kwanthawi za kwanthawi.”

226 Ndi zimenezotu, “nyenyezi,” atumiki asanu ndi awiri amenewo. Atumiki asanu ndi awiri, kudutsa Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo, yomwe ili ndi zaka thuu sauzande.

227 Kuyambira zaka thuu-sauzande zoyambirira, chiwonongeko cha chigumula; zaka thuu-sauzande zachiwiri, kubwera koyamba kwa Khristu; zaka thuu-sauzande zachitatu, za sikisi, ndi Kubwera kwachiwiri kwa Khristu; ndipo Zakachikwi, ndi chimaliziro, mpumulo wa tsiku lachisanu ndi chiwiri.

228 “Kwa mpingo. . .” Oh, kodi mungapirire nane motalika maminiti apang’ono chabe? [Osonkhana akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Tsopano, ine sindikufuna kuti ndikutopetseni inu, koma ine ndiwerenga mofulumira tsopano. “Kwa mngelo. . .” Tsopano penyani, Iye akuyankhula izi molunjika tsopano. Ndipo ife tipita ku Pergamo ndi kukatenga zotsiriza za izo ndiye. . . Ine ndikutanthauza, ku Laodikaya, ndipo kenako ife titseka. Mawa usiku tidzapitiriza kuchokera apa, pa *Chilemba Cha Chirombo*.

*Kwa mngelo wa mpingo wa ku Efeso. . . (Woyamba.)*

229 Tsopano penyani, pamene Yesu anali atayima atakweza manja Ake. Apa pali kanthu kakang’ono kamene ine sindikufuna kuti ndikasiye, kwa inu. Imvani izi. Penyani izi. Iye wayima pakati, pamenepo ndi pakati, pa Zoyikapo Nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide.

230 Tsopano, ngati ine ndikanati ndikuyima *apa*, ndipo zoyikapo nyali zitazungulira, *apa* pa dzanja langa limodzi ndi pamene ine ndinazitulutsa izo, ndipo *apa* pali china, mu chizindikiro cha

mtanda, pakuti zinali kudzera mu mtanda umene unabweretsa Mpingo.

<sup>231</sup> Ndi Uyu wayima apayu; ndi utawaleza pamwamba pa mutu Wake, ngati pangano. “Ine ndapanga pangano Langa ndi Mpingo, kudzera kwa Abrahamu, kudzera Mbewu yake, onse amene ayitanidwa.”

<sup>232</sup> M’bale wanga, usiku wina, akumulandira Khristu, iye anati, “Usamandikakamize konse ine, Bill.” Anati, “Pamene Mulungu akuyankhula ndi ine. . .”

Ine ndinati, “Iwe sungabwere kufikira Iye atakuyitana iwe.”

<sup>233</sup> “Palibe munthu angabwere kwa Ine, pokhapokha Atate Anga atayitana.” Winawake amachita chinachake, amakukokera iwe mmwamba, ameneyo ndi winawake. Koma pamene Mulungu ayankhula, iwe umabwera, mwaona. Uko nkulondola. Atayima pamenepo. . . “Palibe munthu angadze, pokhapokha Atate Anga atamukoka iye.”

<sup>234</sup> Ndi Uyo wayima apoyo, “ukamamuwona ngati mwala wa yaspi ndi sardiyo, woyamba ndi wotsiriza,” Benjimini ndi Rubeni, mbadwa zonse thwelofu. Ndipo momwe, Baibulo, chidutswa chirichonse chimangolumikizana molunjika limodzi monga choncho, chirichonse mwangwirow! Zindikirani pamene Iye wayima pamenepo, kuti ayang’anidwe tsopano, penyani chimene chikuchitika. Iye anati Iye anali “Alfa ndi Omega,” Iye anali “Woyamba ndi Wotsiriza. Iye amene Anali, ndi amene Ali, ndi Amene Adzadza.” Iye anali nazo mdzanja Lake lamanja, tsopano, nyenyezi zisanu ndi ziwiri.

<sup>235</sup> Tsopano apa Iye anayambira ku Efeso, ndipo Iye akuyamba kuyatsa choyikapo nyali. Anachiyatsa pamenepo. Kenako m’badwo wotsatira, ife tikupeza, m’badwo wa mpingo wotsatira, iwo ukuyamba kuzimirira; m’badwo wa mpingo wotsatira ukuzimirira moWonjezera pang’ono; mpaka m’badwo wa mpingo wachinai, zaka fifitini handiredede za mibadwo ya mdima. Ndipo pafupifupi 500, 1500, cha mmenemo, kunayamba kuchita mdima kwambiri mpaka iwo anali kutali, ndipo iwo unatsala pang’ono kuzima.

<sup>236</sup> Ndipo, zindikirani, uliwonse wa mibadwo ya mpingo imeneyo, Iye anati, “Iwe sunakane Dzina Langa. Iwe sunakane Dzina Langa. Iwe sunakane Dzina Langa.” Koma pamene Iye akutulukira ku mbali ina ya mibadwo ya mdima, anati, “Iwe uli nalo dzina lakuti uli ndi moyo, koma ndiwe wakufa.” Iye anali atapanga bungwe. Iye anatenga dzina lina labodza.

<sup>237</sup> Mudzawona, mawa usiku, chimene wotsutsakhristu ali. Iye ali ndi ubatizo wabodza, kukupangani inu kukhulupirira kuti ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Iye ali ndi ubatizo wa madzi wabodza (Inde, bwana.), umene suli wa Mwamalemba nkomwe. Iye ali nazo zinthu zonsezo, zongokwanira kuti azitsanzira, kuti akhale wochenjera ndi woathyathalika.

238 Penyani kumene izo zikuchokerako. Pomwe apo ndi pamene izo zinayambira, umo momwe; zikutulukira mbali yina iyi cha *apa*.

Kenako Iye anati, “Iwe wangotsala ndi Kuwala pang’ono,” Luther.

239 Kenako potsatira kunadzabwera Wesley, ndi momwe izo zinadzakhalira mu m’badwo wake. Izo zinayamba kuwalirapo.

240 Kenako, kuchokera pakati pa m’badwo umenewo ndi m’badwo wotsiriza, Iye anadzayika khomo lotseguka. Iye anayika khomo lotseguka kwa iwo amene akanati adzalowe. Kenako Iye anati, “Iwo unadzapita mu chikhalidwe chofunda.” Ndipo Iye anawulavula iwo kuchokera mkamwa Mwake. Anatenga wotsalira, chiukitsiro chinadzabwera, ndipo kutali Iye anapita ndi iwo. Uko nkulondola.

241 Ndi Uyo apo, atayima mu Zoyikapo Nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide. Tsopano:

*Kwa...mpingo wa Efeso lemba; Zinthu izi... lemba; Zinthu izi zimene anena iye amene wanyamula nyenyezi zisanu ndi ziwiri mdzanja lake lamanja, amene akuyenda pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide;*

242 “Ine ndikudziwa ntchito zako.” Kumbukirani, inu simunaiwalidwe.

*Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi kulimbika kwako, ndi chipiriro chako, ndi...iwe sungathe kupirira nawo iwo amene ali oyipa:...*

243 Ndipo ife timangolekerera chirichonse chimene chiri choyipa, ndi kuchitcha icho chipembedzo. “Oh, chabwino, iwo amapita...Ife timapita ku tchalitchi. Ife ndi abwino monga ena onsewo.” Kupita kunyumba, kukakhala pakhomo Lachitatu usiku ndi kumawonera televizioni, maenje kumene a gehena. Uko nkulondola. Ndi kumatuluka ndi kumakamvetsera ku makanema, owonera uli mgalimoto. Kwatentha kwambiri kuti tipite ku kanema, ngakhale...ku tchalitchi; ndipo ngakhale mlaliki amatseka, mkati mwa chirimwe. Inu mukuti, “Kwatentha kwambiri kuti tipite ku tchalitchi.” Izo sichoncho, zidzakhala zoyipa kwambiri, kupita ku gehena, m’bale. Inu mudzapita, ena a masiku awa, kumene kudzakhale kotentha kuposa zimenezo. Inu kulibwino mumvetsere.

244 Inu mungakwanitse bwanji? M’bale, inu simungaipangitse nkunda kuti idye kavalo wakufa, ngati mungati mutero. Iyo singachite zimenezo. Chikhalidwe chake ndi chosiyana. Nkhunda ilibe ndulu. Iyo singagaye zimenezo.

245 Ndipo munthu amene wabadwa mwatsopano, mwa Mzimu wa Mulungu, sangadye zinthu zimenezo. Iye sangalekerere

zimenezo. Izo zimakhala kunja kwa malingaliro ake. Iye sangachite zimenezo. Iye sangatero.

<sup>246</sup> Inu mukudziwa zimenezo. Mbalame za nthenga zimawulukira limodzi. Ndipo, lero, dziko ndi mpingo ndi zofanana kwambiri, inu. . . Iwo amayankhula mofanana, iwo amamwa mofanana, iwo amasuta mofanana, iwo amatukwana mofanana, iwo amavala mofanana, iwo amachita mofanana. Ndipo iwo, inu simungakhoze kusiyantsa wina kwa mzake, ndipo komabe inu mukuyenera kuti musindikizidwe ndi Mzimu Woyera.

<sup>247</sup> Izo nzamphamvu kwambiri, m'bale, koma, ine ndikukuuzani inu, izo zidzakupatsani inu Moyu.

<sup>248</sup> Panali munthu, nthawi yina, anapita ku gulu la alaliki, kumene iwo anali ndi seminare, yotchedwa sukulu ya aneneri. Ndipo mmodzi wa iwo anati, "Telekani mphika waukulu tsopano. Ife tikhala ndi chakudya chamadzulo." Anati, "Eliya anabwera, mwamuna amene ali ndi magawo awiri kwenikweni."

<sup>249</sup> Chotero mmodzi wa anyamatawo anapita kukatola wina—nandolo wina, ndipo iye anatenga mphonda zaziwisi zodzaza chilolo ndi kuziyika izo mu mphika, ndipo anayamba kuziwiritsa izo. Bwanji, iwo anayamba kudya. Iwo anati, "Muli imfa mu mphikamo." Zimenezo ziri ngati zimene ena a maseminare awa angakhoze kuphika, nawonso. Uko nkulondola. Anati, "Muli imfa mu mphikamo."

<sup>250</sup> Eliya anati, "Dikirani miniti, ife tisamalira zimenezo." Iye akupita ndipo akukatenga ufa wodzaza mdzanja, ndipo akuwponyera iwo mkati, chotero zimenezo zinasintha zinthu. Ufa, nsembe ya ufa, "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," msere-woperedwa mofanana, wa nsembe ya ufa, ndipo izo zinapanga kusiyantsa.

. . . sungathe kupirira nawo *iwo amene ali oyipa:*  
*ndipo unawayesa iwo amene amanena* kuti *iwo*  
*ndi alaliki, kapena, atumwi, ndipo iwo siali, ndipo*  
*wawapeza iwo kukhala onama:*

<sup>251</sup> Icho ndi chimene Iye ananena; ine sindinanene zimenezo. Ine ndikungomubwereza Iye. Koma inu mukudziwa chimene Mulungu amafuna? Mulungu amafuna ubatizo wa Mzimu Woyera, kapena inu mwatayika.

<sup>252</sup> Ndipo munthu amachoka kuno ali ndi ma D.D.D. angapo, ndi ma L.D., ndi ma Ph.D., ndi Digrii ya Batchala, ndi china chirichonse kumbuyo kwa zimenezo, ndipo nthawizina osadziwanso mochuluka za Mulungu kuposa kanthu. Izo nzoona. M'bale, zimenezo sizikutanthauza kalikonse. Koma dziko lonse limati, "Chabwino, mtumiki wathu ndi Dokotala wa Zauzimu." Oh, chifundo. Zimenezo ziribe chochita chirichonse ndi Mulungu kuposa—kuposa kumwa madzi; osati kwambiri. Uko nkulondola. Mulungu samasamala kuti ndi ma Ph.D.



angati, kapena ma D.D. Ndipo—ndipo inu mukudziwa chimene Baibulo limachitcha... Tsopano, iyi si nthabwala, chifukwa ine sindimakhulupirira mu kunena zimenezo. Koma Baibulo limatcha D.D., “galu wakufa.” Ndicho ndendende chimene Baibulo linanena kuti izo zinali, “galu wakufa.” Chabwino, anati, “Iwo sangathe kuuwa.” Chotero, ndiye, chabwino.

*Ndipo wakhala, ndipo uli ndi chipiriro, ndipo chifukwa cha dzina langa...*

253 Oh, ine ndikufuna kuti ndiperere zimenezo mkati, kuti inu muzimvetse zimenezo mmausiku angapo, Mulungu akalola.

*...wagwira ntchito, ndipo sunakomoke.*

254 “Inu munakhala kumene ndi Iwo.” Chabwino. Zindikirani.

*Komabe ine ndiri ndi zinthu zina zotsutsana ndi iwe,...*

255 Tsopano, apa ndi pamene ine ndikuyenera kusiyira tsopano, kwa kanthawi pang’ono, mpaka ine nditazipeza izi pomwe apa kuti tidzathe kuzimvetisa izo mawa usiku.

*...ndiri ndi zinthu zingapo zotsutsana ndi iwe, chifukwa iwe wasiya chikondi chako choyamba.*

256 Vuto ndi chiyani ndi kachisi? Munthu ayenera kuti azikwanitsa kunena kuti, pamene inu mukumana ndi munthu, “Kodi zokuchitikirani zanu za Chikhristu, ndi liti limene izo zinali zokondweretsa kwambiri kwa inu?”

Inu mukuyenera kuti muzikwanitsa kunena kuti, “Pakali pano!”

257 “Chabwino, chondichitikira changa chopambana chinali mmbuyo pamene ine ndinalandira koyamba ubatizo wa Mzimu Woyera, pamene ine ndinabwera.”

258 Kenako muziti, “Oh, m’bale, inu mwagwa kuchokera ku chisomo.” Uko nkulondola. Penyani.

*...wasiya chikondi chako choyamba.*

Kuwonetsera kuti iwo anali ndi chinachake pachiyambi, ndipo anachisiya icho.

259 “Osati iye amene ayamba; koma iye amene apirira kufikira kumapeto, yemweyo adzapulumutsidwa.” “Osati iye...onse amene anena, ‘Ambuye, Ambuye,’ koma iye amene achita chifuniro cha Atate Anga.” Oh, ndiroleni ine ndingolola izo zilowerere maminiti pang’ono chabe. Ine ndimayankhula mwaliwiro usikuuno, mulimonse, chotero tiyeni ife tilole izo zilowerere maminiti pang’ono chabe, mwaona. “Iye amene achita chifuniro cha Atate Anga.” “Iye amene apirira mpaka kumapeto. Iye amene apirira!”

260 Ngati winawake anena kuti, “Ine ndikumukhulupirira iye, munthu ameneyo, ndi wachinyengo wakale.”

<sup>261</sup> “Chabwino, ngati inu mukuganiza zimenezo za ine, ine ndisiya tchalitchi. Ine sindikhalanso ndi chochita ndi icho.” Chabwino, ndi zimenezotu. Mukuona? Zikuwonetsera chimene inu mwapangidwa nacho. M’bale, ngati iye anali tirigu kuyamba ndi kuyamba, iye adzakhala tirigu kumapeto. Kungoti inu simunakhale utali wokwanira pansi kuno. Inu simudzachikonza konse chinthucho. Uko nkulondola.

*Chotero kumbukirani kumene inu mwagwera, . . .*

<sup>262</sup> Bwererani ndipo mukakumbukire pamene inu munkakhala ndi zokuchitikirani pamene inu simunkayankhula za aliynense. Chirichonse chikalakwika mu tchalitchi, inu simunkakhala pa masitepe a woyandikana naye wanu kumeneko ndi kumayankhula za tchalitchi, ndi kuyankhula za wina aliynense, kuchokapo ndi kupita kukajowina tchalitchi china. Ayi, inu munkakhala pomwepo, moleza mtima ndipo munkapempherera izo, ndipo Mulungu ankazidutsitsa izo, mwaona.

*Kumbukirani . . . kumene inu mwagwera, ndipo mulape, . . .*

<sup>263</sup> Inu mukudziwa chimene “kulapa” kumatanthauza, sichoncho inu?

*. . . ndipo chitani ntchito zanu zoyamba; . . .*

<sup>264</sup> Bwererani ndipo mukapeze chokuchitikirani chanu choyamba. Mukachite zinthu zimene munkachita poyamba. “Mupite mpaka pa guwa ndipo mukakonzane izo ndi Mulungu,” mwa kuyankhula kwina. Uko nkulondola.

*. . . kachiteni ntchito zanu zoyambirira; kapena ine ndidzabwera kwa inu mwamsanga, ndipo Ine ndidzachotsa choyikapo nyali chanu kuchichotsa pamalo pake, pokhapokhapo ngati inu mulapa.*

<sup>265</sup> Uh-huh, “Ngati inu simutero, inu mudzakhala ndi tchalitchi chosweka, ndi kukhala zidutswa, pokhapokhapo ngati inu mulapa.”

<sup>266</sup> “Koma ichi inu . . .” Oh, tsopano apa ife tikubwera. Gwiritsitsani mwamphamvu. Mvetserani mwatcheru. Valani singileti yanu yachipembedzo tsopano, ndipo mutsitse ambulera wanu. Tamvetserani. Za . . .

*Koma ichi inu muli nacho, kuti inu mudana nazo ntchito za Chinikolai, zimene inenso ndimadana nazo.*

<sup>267</sup> “Inu mumadana ndi ntchito za Chinikolai.” Tsopano penyani. Kodi “ntchito” zinali chiyani mu Efeso, mu m’badwo wa mpingo wotsatira, zinali “chiphunzitso.” Ife tidzapitiriza zimenezo, mawa usiku, “Chinikolai.”

*Ndipo iye amene ali ndi khutu, amve chimene Mzimu anena kwa mipingo; Kwa iye amene agonjetsa Ine*

*ndidzampatsa kuti adzadye za mtengo wa moyo, umene  
uli pakati pa paradiso wa Mulungu.*

268 Tsopano, yotsatira, ndime yotsatira ikuyamba ndi Mpingo wa Smurna.

269 Tsopano, “Chinikolai,” ndi pamene ife titi tidzayambire, mawa usiku, kuchotsedwa mu Chivumbulutso 13. Unsembe wa Chinikolai, momwe iwo unayambira pomwe apo mu Efeso. Ndipo pamenepo ndi pamene m’badwo wa mpingo umenewo unalepherera, mu zaka firii handirede za kukhalapo kwake. Iwo usanachoke mu kukhalapo, Achinikolai anayamba kuyambitsa chiphunzitso, unsembe wa abale.

270 Ndiyeno, choyamba, icho chinachokera kwa Nikolasi, amene anali mmodzi wa a—atu—. . . mmodzi wa. . . ndi iye. . . Mu Machitidwe mutu wa 6, ine ndikukhulupirira, ndi ndime ya 5, pamene iye anapita ndipo anakasankha madikoni. Ndipo iwo anamutenga uyu, amene anali Nikolasi kumeneko, ndipo anayambira kumeneko ndipo anachitcha icho Chinikolai, ndipo anayamba kupanga bungwe unsembe. Ndipo kuchokera pamenepo zinakhala “ntchito,” zomwe iwo ankachita, kumanena zinthu izi pa kuvomereza, ndi zina zotero. Ndipo kenako izo zinadzakhala “chiphunzitso” kuno, ndipo zinapita ku Babeloni. Ndipo zinadzathera kumusi kuno, pa nthalwi yotsiriza, ndi Chikhristu chonse chitakulungidwa pa izo; otsalira pang’ono okha kuti apulumutsidwe kuchokera mmenemo. Penyani ndipo muwone chimene izo ziri, mawa usiku, ngati Mulungu alola.

271 Oh, m’bale wanga wokonedwa, mlongo wanga wokonedwa, kwa Iye amene angathe kukutetezani kuti musagwe, kwa Iye amene ali wokhoza kugwira mtima wanu mu chisomo, mulole Iye atsanulire madalitso Ake pa inu. Inu musadzaiwale konse kuti ife tikukhala mmasiku otsiriza a m’badwo wa mpingo wotsiriza, kumene iwo unanenedweratu kuti udzakhala m’badwo wa mpingo wofunda, mtima-watheka chabe za Iwo. Ndipo musiye kukhala a mtima-watheka. Bwerani kwenikweni kwa Khristu, ndi mtima wanu wonse.

272 Ine sindikukuuzani inu mpingo woti mujowine. Izo ziribe. . . Mulungu sadzakufunsani zimenezo pa Chiweruzo. Ayi, bwana. Iye samasamala kuti ndinu a mpingo wanji.

273 Iye akufuna *inu*; ndi munthu payekha. Ndipo inu mukuyenera kubadwa mwatsopano ndi kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera, kapena inu mwapita. Mukuona? Inu mukungosewera tchalitchi, inu mukungotsanzira, kufikirira inu mutakhala nacho kwenikweni chokuchitikirani cha kubadwa mwatsopano.

274 Ndipo pamenepo, Iye amene anayima pamenepo, ndi Zoyikapo nyali Zisanu Ndi Ziwiri Zagolide, kudutsa mu Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo, ndipo Mzimu Woyera

womwewo umene unayatsa Mpingo kumeneko, ukuyatsa Iwo pano.

<sup>275</sup> Tsopano, pakhala pali otsanzira mu mpingo umenewo, ndipo Achinikolai awa kumeneko, ndi onse kudutsa mu m'badwo wa mpingo uliwonse, otsanzira, mpaka izo zikufika pansi apa mpaka izo zangokhala ndi mgwirizano umodzi waukulu wa bungwe. Ndipo Mulungu akukankhira chinthu chonsecho panja, ndipo akuwatengera otsalira a anthuwo ku Ulemelero.

<sup>276</sup> Ambuye akudalitseni inu. Izi ndi zakhala ngati zokandapala, abwenzi, koma ndizabwino. Izo zikuthandizani inu ndi kukutetezani inu kuti musagwe. Tsopano, musapite mozungulira, kumakati, "M'bale Branham anawuzazira mpingo wanga." Izo sizinali za mpingo uliwonse. Izo zinali kokha za inu, monga munthu payekha. Ine sindi. . .

<sup>277</sup> Ngati inu muli wa mpingo wa Baptisti, ndiye inu mukhale wa Baptisti weniweni wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ngati inu muli wa mpingo wa Methodisti, mukhale wa Methodisti weniweni wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, chirichonse chimene chiri. Ndipo inu simudzakhala ndi ngongole; inu mudzakhala chopindula ku mpingo uliwonse, kapena oyandikana nawo aliwonse, kwa ulemelero wa Mulungu.

Ambuye akudalitseni inu tsopano, pamene ife tikuimirira, ngati inu mungathe.

<sup>278</sup> Wokonedwa Mbuye wa Moyo, titatha kuwerenga Mawu Anu, ife tayima mwamantha. Pozindikira kuti tsiku lina kuwerenga uku usikuuno kudzakhala. . .Ife tidzazimva Izo pa tepi yojambulidwa, monga izo zinkamvekera, pa Tsiku la Chiweruzo. Kodi ife tidzachita chiyani za izo? Powona kuti ife tikukhala mu m'badwo wotsiriza uno, mdimaponseponse, ndi nthawi yotani. Kuwona Kudza kwa Ambuye, zizindikiro zikuwonekera, "mafunde aakulu akugudubuzika; mitima ya anthu ikulephera, mantha; kusokonezeka kwa nthawi; kupanikizika pakati pa mafuko."

<sup>279</sup> Ambiri amati, "Oh, ine ndazimvapo izo kwa zaka." Koma kodi Lemba silinanene kuti iwo akanadzanena zimenezo, "Palibe kusiyana mu nthawi kuposa pamene makolo athu anagona"? Osadziwa kuti ife tiri pa chiundo kumene. Iye akhoza kubwera mmawa usanafike.

<sup>280</sup> Ndipo, Atate, ndi tsiku lanji kapena ora lanji, ife tikudziwa, kuti ulusi wawung'ono uwu wamoyo umene tikuyendapo udzatidukira pansi pathu. Miyoyo yathu yosauka izidzalendewera kutali pa muyezo, pa Mawu a Mulungu, ndi mmene tikuchitira pa zimene ife tamva ndi kuwerenga.

<sup>281</sup> Izo zikutikakamiza ife, Ambuye, kuti tiyime tsopano ndi kudzifufuza tokha. Ndipo pamene amuna ndi akazi, anyamata kapena atsikana, ayima pano mwa omvetsera apang'ono awa, usikuuno, oganiza bwino ndi amphamvu, mulole iwo

aganize mwakuya pakali pano. Ndipo ngati iwo sanabadwebe mwatsopano, mulole iwo alingalire mmitima yawo pakali pano, “Ine sindidya kapena kumwa mpaka Inu mutandidzaza ine ndi mana omwewo amene Inu munawadzaza nawo iwo pa Tsiku la Pentekoste. Mpaka dziko litakhala lakufa, ndipo chirichonse nkukhala chachiwiri kupatula Inu, Ambuye Wanga, ndi chikondi cha china chirichonse chidzazimirira. Koma muchotse chikondi chonse cha mdziko kwa ine, ndipo mudirole ine kuyambira lero ndikhale Wanu mwathunthu.” Perekani izi, Ambuye.

<sup>282</sup> Khalani ndi anthu pamene akupita ku nyumba zawo. Mukumbukire osowa, O Mulungu, osauka mdziko lathu, osauka mu mzimu, iwo amene ali ndi njala.

<sup>283</sup> Mulungu, ukitsani atumiki, konsekonse. Muwadzaze iwo ndi Mzimu Woyera, ndipo muwatume iwo, akalalikire, Ambuye, ngati makombola. Ife sitikudziwa kuti ndi ora lanji... Ife tinangodutsa njira iyi kamodzi. Ife tinangokhala chivundi kamodzi, ndipo mathokozo akhale kwa Mulungu chifukwa cha zimenezo. Koma, moyo winawo, ife sitidzalalikira Uthenga mu moyo winawo umene uli nkudza; koma ife tidzakakondwera mu Uthenga, pamodzi ndi iwo a mibadwo amene anawulandira Iwo; ndi Woyang’anira Wamkulu, Ambuye wathu Yesu Amene ali woyenera, ndipo matamando onse akhale kwa Iye kwanthawi za nthawi. Amen.

<sup>284</sup> Mulungu akudalitseni inu. Tembenukani ndipo mugwirane chanza wina ndi mzake, pamene ife tikuyimba *Chodala Chikhale Chimango Chimene Chimamanga*, ngati inu mungathe.

Chodala chikhale chimango chimene  
chimamangiriza  
Mitima yathu mu chikondi cha Chikhristu;  
Chiyanjano cha malingaliro apaubale  
Chiri chonga chija Chakumwamba.

Pamaso pa Mpandowachifumu wa Atate  
wathu,

<sup>285</sup> Tsopano, gwiranani chanza wina ndi mzake. Ndi maminiti teni okha, nthawi, pakuti kuwala tsopano kukulandirana kuyaka. Inu nonse mugwirane chanza, pitani kwanu, mukusangalala, ndipo mudzabwerere mawa usiku. Ikamadzakwana hafu-seveni, ndendende, ife tidzakhala tikuyamba msonkhano, Mulungu akalola. Nzodabwitsa bwanji...?...



*MIBADWO ISANU NDI IWIRI YA MPINGO* CHA54-0512  
(The Seven Church Ages)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu madzulo, Meyi 12, 1954, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)